


YEHOVA-YIRE ¹

 Tiyeni tingokhalabe chiyimire kamphindi pamene ife tikuweramitsa mitu yathu ku mawu a pemphero. Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, ine ndikudabwa usikuuno ndi angati akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, muli ndi chinachake pa mtima wanu chimene mukufuna kuti Mulungu akuchitireni, mungokweza mmwamba manja anu. Ambuye apereke zopempha izi tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu ndi mitima yathu pamaso pa Iye.

² Atate athu Akumwamba, ife tikuyandikira Mpandowachifumu Wanu wa Chisomo kenanso, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wamkulu wa Mulungu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mwayi wobwera ndi chitsimikizo kuti Inu mumva ndi kuyankha chimene ife tikupempha. Ife tikupemphera, Atate, kuti Inu mukhululukire machimo athu, ndiko, kusakhulupirira kwathu. Ndipo, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mutipatse ife chikhulupiriro, chikhulupiriro chochuluka usikuuno. Ndipo Inu mukudziwa chimene chinali kuseri kwa dzanja lililonse apo, pansi mu mtima. Iwo amafuna chinachake, Ambuye. Iwo anakweza dzanja lawo molemekeza, akuyembekezera chinachake kuchokera kwa Inu. Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, chirichonse chimene icho chinali, kuti icho chiperekedwa kwa anthu.

³ Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha kutichezera usiku watha. Tikupemphera kuti Inu mubwerere kwa ife usikuuno ndi kuchuluka kwa mphamvu ndi chisomo, ndipo mudzapereke kwa ife zokhumba za mtima wathu, pakuti, zoonadi chokhumba chathu ndi kuchita Chifuniro Chanu ndi kuwona Chifuniro Chanu chikuchitika. Ndipo ife tikudziwa chimene Chifuniro Chanu chiri zokhudza odwala, kuti Inu munakwapulidwa pa nsana Wanu chifukwa cha machiritso athu, “Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ndipo, Atate, ife tikupemphera kuti—kuti Chifuniro Chanu chachikulu chichitidwe usikuuno, kutipatsa ife chikhulupiriro kuti tikhulupirire izo, mwa unyinji, kuti wodwala aliynense achiritsidwe, ndipo munthu aliynense amene ali wotayika akhoze kukumbukira kuti Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Perekani izi, Ambuye.

⁴ Mulole iwo adziwe kuti bola ngati pali a—Nsembe yamagazi Pamenepo kwa iwo, machimo awo sangawonedwe ndi Mulungu. Koma ngati iwo angafe popanda kuvomereza Iyo poyera ndi kuyilandira Iyo, ndi kubadwanso mwatsopano, sipangakhale njira iliyonse yoti iwo alowe mu Ufumu. Ndipo mulole uwu ukhale usiku umene munthu aliynense wochokera pansi pa Magazi akhoze kupita mofulumira pansi pa Magazi

usikuuno, mu Dzina la Ambuye Yesu. Ndipo ife tikupatsani Inu matamando. Amenii.

⁵ Mwayi waukulu kwambiri kukhala pano usikuuno ndi kuyankhula kenanso. Ndipo usiku watha ife tinali ndi nthawi yodabwitsa chotero, kuchezeredwa ndi Ambuye. Koma ndinakusungani inu mochedwa kwambiri. Ine ndinalephera kuti ndiyigwire nthawi, mwanjira ina.

⁶ Zikukhala ngati tinatsala pang'ono kukhala ndi dzuwa lambiri lero. Ine ndinali. . . Mwana wanga wamng'ono, Joseph, wakhala akundivutitsa ine kuti apite kosambira. Chotero malo amene ife tikukhala ali ndi dziwe laling'ono, lokhala ngati lotchingidwa kumbuyo uko, ndipo iye anati, "Bwerani, mudzandiwone ine, adadi. Ine ndikhoza kusambira."

Ine ndinati, "Chabwino."

⁷ Ine ndinapita kumeneko mmawa uno, ndinatenga Baibulo langa, ndi zina. . .kuti ndizikalemba zolemba zina. Ndipo pamene ine ndimawerenga, iye. . .apa iye anabwera atavala zovala zosambira zake zazing'ono, anati, "Muzindiwona ine, adadi, ndikhoza kulumphira!" Chabwino, ngati ine ndinayamba ndawonapo chule akulumphira mmadzi! Ndipo iye anadzatulukamo, ndipo madzi akutuluka mmphuno zake ndi mkamwa, iye anati, "Ine ndachita bwanji?"

Ine ndinati, "Iwe ukuchita bwino."

⁸ Ndipo ine ndinangoyamba kuganiza za nthawi ina imene ine ndinanena chinthu chomwecho kwa abambo anga. Dziwe laling'ono lakale, tisanapite ku mtsinje, panali dziwe, ndipo anafe tinkayenera kuchotsa zinyalala zobiriwirazo mu ilo, ndipo tinka. . .madzi sanali opitirira pafupifupi mainchesi sikisi kuya kwake. Ndipo ndinapitirira kuwauza bambo anga, "Ine ndikhoza kusambira."

⁹ Chotero Lamlungu lina masana iwo anapita kumeneko. Ndipo iwo anali ndi kabokosi kakang'ono ka sopo kali pamenepo. Ndipo ine ndinabwerera mu tchire ndipo ndinavula zovala zanga, chimene chinalipo kuti ndivule; kungokoka msomali umodzi, inu mukudziwa. Ndipo ndi angati anayamba awonapo umodzi woterowo? Ine ndikuwona. Kungovala ovololo, yopanda zingwe; basi ndi—twayini mopingasa, ngati zingwe, ndipo kenako msomali basi. Kungokoka msomali ndipo, ndizo zonse zimene ukuyenera kuchita, nkulumphira mmenemo. Ndipo chotero ine ndinakwera pa bokosi ili ndi kugwira mphuno yanga, inu mukudziwa, ndipo ndinalumphira mmenemo, ndipo matope anawulukira motalika *choncho*. Abambo anga atakhala pansii apo, akundiayang'ana ine. Ine ndinati, "Ine ndikupanga bwanji?"

¹⁰ Anati, "Choka mmenemo ndipo upite ukasambe!" Ndimaganiza kuti zakhala nthawi yayitali bwanji zimenezo!

¹¹ Ndipo, inu mukudziwa, nthawi imangothawa kuchokera kwa ife, sichoncho iyo? Ife tiribe nthawi basi, zikuwoneka ngati, panonso, kuti tizichita zinthu. Ndipo nthawi sikuyembekezera aliyense. Chotero tiyenera tizigwira ntchito momwe ife tingathere, chifukwa ora likudza pamene m’badwo uwu udzapita, ndipo padzakhala kam’badwo kena kakubwera, ngati kuli kam’badwo kena. Moonadi, ndikunena izi ndi mtima wanga wonse, (ine sindikudziwa kuti Iye abwera liti; palibe aliyense wa ife akudziwa), koma, moon, sindikukhulupirira kuti padzakhala kam’badwo kena. Ine ndikukhulupirira Khristu adzabwera mu kam’badwo kano. Ine sindikudziwa kuti ndi liti, tsopano, izo zikhoza kukhala usikuuno kapena zikhoza kudzakhala zaka teni kuchokera pano, kapena twente, koma ndikukhulupirira Iye adzakhala mu kam’badwo kano. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ngati Iye satero, ine ndikufuna kuti ndizikhala moyo ngati kuti Iye atero, mulimonse, chifukwa ine ndikudziwa kuti ilo likhoza kukhala tsiku langa lotsiriza, kapena tsiku lanu lotsiriza.

¹² Ndiyeno, muzikumbukira, ngati tingapite Iye asanabwere, ife tidzakhala tiri mmwamba ndipo mu Kukhalapo Kwake, kapena, tidzawukitsidwa ena asanasinthidwe. “Lipenga la Ambuye lidzalira, akufa mwa Khristu adzawuka poyamba. Kenako ife amene tiri moyo ndipo tatsalira tidzasandulika mkamphindi, mu kuthwanima kwa diso, ndi kudzakwatulidwa limodzi ndi iwo, kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga.” Tayang’anani pa dongosolo la chiwukitsiro. Mwaona, Mulungu akudziwa kuti tikufuna kudzawawona okonedwa athu. Ndipo ngati titakafika kumeneko ndi kukumana naye Iye poyamba, ife tingakakhale tikuyang’ana yang’ana kuti tiwone ngati amayi kapena abambo ndi ena onse a iwo ali kumeneko. Koma mukuona momwe, Mzimu Woyera mu nzeru Zake? Ife tidzakumana kaye wina ndi mzake poyamba, ndipo kenako tikadzafika kumeneko ndi kumadzayimba *Chisomo Chodabwitsa*, pamenepo ndi pamene padzakhale nthawi yopembedza. Inu mukuganiza kuti ine ndimachita moseketsa tsopano, mudzandiwone ine Kumeneko! Idzakhala nthawi yopambana kwa ine ndi tonse a ife tikadzafika Kumeneko.

¹³ Tsopano tiyeni tiwerenge zina kuchokera mu Baibulo lakale lodalitsidwa apa usikuuno. Tiyeni titsegule ku Aroma, mutu wa 4, ndipo tiwerenge gawo chabe la Bukhu la Aroma. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge malo awiri usikuuno, kuchokera mu Genesis ndi kuchokera mu Bukhu la Aroma. Tsopano mu Bukhu la Aroma, mutu wa 4, ndime ya 17.

(Monga kunalembedwa, ndakupanga iwe tate wa mafuko ambiri,) pamaso pa iye amene iye anakhulupirira, ngakhale Mulungu, amene apereka moyo kwa akufa, ndi kuzitcha zinthu zimene kulibe monga ngati kuti ziripo.

Amene popanda chiyembekezo anakhulupirira mwa chiyembekezo, kuti akakhale tate wa mafuko ambiri; monga mwa icho chimene chinalembedwa, Chotero mbewu yako idzakhala chomwecho.

Ndipo posakhala ofooka mchikhulupiro, sanaganizire thupi lake lomwe linali lakufa, pamene iye anali pafupifupi usinkhu wa zaka handiredede, ngakhalenso . . .kuwuma kwa mimba ya Sarah:

Iye sanagwedezeke pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira; koma analimbika mu chikhulupiro, akupereka ulemelero kwa Mulungu;

Ndipo pokhala wokhutitsidwa kwathunthu kuti, chimene iye analonjeza, iye anali wokhoza kuchichita.

Ndipo chifukwa chake ichi chinawerengedwa kwa iye chirungamo.

Tsopano ichi sichinalembedwe kwa iye yekha, kuti chinawerengedwa kwa iye;

Koma kwa ifenso, kwa iye amene kudzawerengedwa, ngati tikhulupirira pa iye amene anawukitsa Yesu Ambuye wathu kwa akufa;

Amene anaperekedwa chifukwa cha cholakwa chathu, ndipo anawukitsidwa chifukwa cha kulungamitsidwa kwathu.

¹⁴ Oh, momwe ine ndimazikondera Zimenezo! Limenelo ndi Lemba langa limene ndimakonda kuliwerenga la Baibulo, chifukwa ndi chenicheni kwambiri chimene Mulungu anali, chimene Iye analonjeza ndi kulumbira kuti Iye akanadzachita. Ndipo tsopano ine ndinasankha phunziro ili chifukwa ine ndikuganiza kuti pa msonkhano uliwonse, kuwona chikhulupiro chimene ife tinachiwona chikuchitidwa pano usiku watha, kuti panalibe munthu wofooka pakati pathu koma amene anachiritsidwa. Chimene mphamvu ya Mulungu inadza ndi chimene Iye anachita! Kenako ndinaganiza, ngati tingamange mozungulira chinachake chenicheni, kupanga a—chopindula kukhala cholingacho, ndiye zikanakhala zopambana bwanji pamene ife tikanatha kugunda usiku waukulu uwo kapena ora la pachimake.

¹⁵ Ndipo tikuyenera kukumbukira kuti palibe chimene chingachitike popanda chikhulupiro, ndipo poyamba chikuyenera kuvomerezedwa. Pakuti Iye ndi—Iye ndiye Mwini wa chikhulupiro, ife tikudziwa zimenezo, ndipo palibe chimene chingachitike popanda chikhulupiro. Ndipo popanda chikhulupiro ndi zosatheka kumukondweretsa Mulungu.

¹⁶ Ndipo tsopano Iye ndi Wansembe Wamkulu wa kuvomereza kwathu. Tsopano a—King James apa, mu Bukhu la Ahebri, akuyika izo ngati “kunena.” *Kunena* ndi *kuvomereza* ndi

chinthu chomwe chomwecho, kunena ndi kuvomereza. *Kuvomereza* kumatanthauza “kunena chinthu chomwecho”: “Ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa,” mwaona, “Tsopano ndi Moyo Wake ine ndapulumsidwa.” Ndipo tsopano ndiye, choyamba, ife timayenera kuvomereza zimenezo; ndipo Iye amakhala ngati Mkhalapakati, ndipo Mkhalapakati yekhaya pakati pa Mulungu ndi munthu, ndipo Iye amakhala pamene kuzipanga kupembedzera pa chimene ife tikuvomereza kuti Iye wachita. Ndi a—ndi chomveka bwino bwanji, chinthu chogwirika chimene icho chiri!

¹⁷ Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba lina, lopezeka mu Bukhu la—Genesis, mutu wa 22, ndipo tiyeni tiyambe kuwerenga apa pa ndime ya 7.

Ndipo Isaki ananena ndi Abrahamu atate wake, ndipo anati, atate Wanga: ndipo iye anati, Ndine pano, mwana wanga. Ndipo iye anati, Taonani moto ndi nkhuni: koma alikuti mwanawankhosa wa nsembe-yopsyereza?

Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzadzifunira yekha mwanawankhosa wa nsembe yopsyereza: chotero iwo anapita awiri onse pamodzi.

Ndipo iwo anafika pamalo amene Mulungu anamuwa iye; ndipo Abrahamu anamanga guwa pamene, ndipo anayika nkhuni mu dongosolo, ndipo anamumanga Isaki mwana wake, ndipo anamugoneka pamwamba pa—pa guwa pa nkhuni.

Ndipo Abrahamu anatambasula dzanja lake, ndipo anatenga mpeni kuti amuphe mwana wake.

Ndipo mngelo wa AMBUYE anamuyitana iye kuchokera kumwamba, ndipo anati, Abrahamu, Abrahamu: ndipo iye anati, Ndine pano.

Ndipo anati, Usaike dzanja lako pa mwanayo, usamuchitire iye kanthu kalikonse: pakuti tsopano ndadziwa kuti iwe—kuti iwe umawopa Mulungu, ndi kuwona iwe... sunandikanize mwana wako mmodzi yekhaya.

Ndipo Abrahamu anatumula maso ake... ndipo taonani pambuyo pake nkhosa yamphongo yogwidwa mu tchire ndi nyanga: ndipo Abrahamu anapita ndipo anakatenga nkhosa yamphongoyo, ndipo anayipereka iyo pa... ngati nsembe yopsyereza mmalo mwa mwana wake.

Ndipo Abrahamu anatcha dzina la malowo, Yehova-yire: monga zimanenedwa mpaka tsiku la lero, Mu phiri la AMBUYE zidzawoneka.

¹⁸ Chimene ine ndikufuna kuti nditenge phunziro pamene, ngati ilo lingatchedwe phunziro, *Yehova-Yire*, mawuwo

amatanthauza “Ambuye adzadzifunira Yekha nsembe.” Ngati Iye alibe imodzi, Iye akhoza kupereka imodzi. Ndine woyamikira kwambiri chifukwa cha zimenezo. Tsopano phunziro lalikulu ili! Ndipo tsopano kuwerenga pamenepo, kuti “Abrahamu sanagwedezeke pa lonjezo mwa kusakhulupirira; koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu.”

¹⁹ Tsopano, Abrahamu anali mmodzi amene Mulungu anapangana naye pangano ndi lonjezo; ndipo Abrahamu, osati iye yekha, koma Mbewu yake ya pambuyo pake, “Abrahamu ndi Mbewu yake.” Ndipo tsopano kumbukirani ichi tsopano. Ngati tikhala akufa mwa Khristu, ndife Mbewu ya Abrahamu ngati tabadwanso mwatsopano. Tsopano, tiyeni tikhale osamalitsa kwenikweni za izi tsopano pamene tikuphunzira phunziro ili. Ndipo tsopano ngati inu mungamvetsetse mwacheru, ine ndikutsimikiza Mzimu Woyera uwulula kwa inu. Inu mugwira chiyembekezocho, ndipo kenako chiwalitsa mzinda uno ndi chirichonse chokuzingulirani, ngati titangotenga nthawi yathu ndi kugwira lingalirolo, chimene Mzimu Woyera ukuyesera kufikitsa kwa ife. Tsopano, Abrahamu, woyitanidwa, amene anapatsidwa lonjezo, kwa Abrahamu ndi Mbewu yake.

²⁰ Tsopano ziripo zochuluka kwambiri lero, abwenzi, zimene zimatchedwa Chikhristu, zimene si Chikhristu.

²¹ Tsopano, ine ndimadana ndi kunena izi. Koma ine zingakhale bwino kuyima pano ndi kukhala wotchuka kwenikweni pakati pa anthu, ndipo—ndipo aliyense nkumakusisita iwe pa nsana pako, ndi chirichonse monga choncho. Komano ine ndikuyenera kuti ndidzakomane nalo gulu limenero pa Chiweruzo, kuti ndidzakayankhire izo. Chotero ine—ine ndikungoyenera kukhala woona mtima.

²² Tsopano ife tikhoza kuyang’ana pa osonkhana, ndi pa dziko lero, pa chimene chimatchedwa Chikhristu, ndipo nkudzapeza kuti izo ndi mailosi milioni kutalikirana ndi Chikhristu. Ndipo zinanenedweratu mu Baibulo kuti zidzakhala mwanjira imeneyo. Tsopano ambiri amavomereza Khristu mwanjira yakuti, “Chabwino, ine ndimamukhulupirira Iye.” Bwanji, mdierekezi amakhulupirira chinthu chomwecho. Mukuona? Ndipo ambiri a iwo amayesetsa kuvomereza izo mongotengeka, kuti, “Chabwino, ine ndinayankhula ndi malirime. Ine ndinavina mu Mzimu.” Ine ndawonapo asing’anga akuchita chinthu chomwe chomwecho, ndi ovina a mdierekezi mu Afrika; ndithudi, kumayankhula mmalirime, ndi kumamwa magazi kuchokera mu chigaza cha munthu, ndi kumaitanira pa mdierekezi. Amayi anga ndi Mmwenye, Mmwenye watheka, ndipo—ndipo anthu awo. Ndinawawonapo iwo akutenga pensulo ndi kudzaigoneka iyo pansu monga *choncho*, ndi kuiwona pensulo ikuthamanga ndi kudzalemba mmalirime osadziwika, iwo atayima pamenepo ndi kumatanthauzira iwo, akuitanira pa mdierekezi. Ndithudi. Mwaona, inu simungapite

ndi zomverera. Mwaona, moyo wanu umene inu mumakhala umachitira umboni chimene inu muli. Mukuona? Ziribe kanthu mtundu wanji wa zogirigisha, inu simungakhazikitse Chikhristu pa zogirigisha zirizonse.

²³ Ndi moyo! Yesu anati, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Osati ndi zodzinenera zawo, osati ndi zimene iwo amanena. Ndipo Yesu nayenso anati, “Mumandiyandikira Ine ndi milomo yanu, koma mtima wanu uli kutali ndi Ine.” Ndiko, ndiko kudzinenera kwawo. Mwaona, moyo wanu umanena zimenezo. Ndipo ngati munthu anena kuti amakhulupirira Mulungu, ndipo nkukana Mawu amodzi a Baibulo ili, kapena nkuwasintha Iwo mwanjira iliyonse, bwanji izo zikuyenera kukhala zolakwika.

²⁴ Inu mukuti, “Izo sizipanga kusiyana kulikonse za zinthu zazing’ono izi.” Izo ndithudi zimatero.

²⁵ Mawu amodzi aang’ono ndi amene anatitengera ife mmavuto onsewa; osati kusawakhulupirira Iwo, koma kungowayika molakwitsa Iwo. Eva anangomupangitsa Satana kuphonyetsa, kungomupatsa iye kulingalirapo. Kumusi kwa M’bale Williams, ine ndangomaliza kumene kudutsa mu izo uko mu Santa Maria. Ndicho chinthu chimene chinatitulutsa ife kuchokera mmunda wa Edeni, ndipo chinayambitsa mwana aliyense wodwala. Monga, ine ndinapempherera mwana wamng’ono wakugwa atagona pamenepo, mphindi pang’ono zapitazo, ndikulowa mkati. Nchiyani chinayambitsa zimenezo? Chifukwa Eva sikuti sanawakhulupirire Iwo konse, koma iye anangolingalirapo, kuti zikanakhala zomveka kuti izi zikhala bwino. Ndipo izo zinayambitsa imfa iliyonse, matenda aliwonse, chisoni chirichonse, kupweteka kwa mtima kulikonse. Ndipo kodi ife tidzabwereramo bwanji? Ngati izo zinapangitsa—ngati izo zinapangitsa zaka sikisi sauzande za izi, kodi ife tidzabwerera bwanji ndi chirichonse chocheperapo kuposa Mawu angwiwo aliwonse momwe Iwo analembedwera?

²⁶ Mdierekezi anapambana nkondoyo pa mtundu wa anthu pokambirana ndi mtundu wa anthu. Kungolingalira chabe, “Bwanji, izo nzoti tizilingalira kuti izi zikhala chiyani? Izo nzoti tizilingalira.” Ngati kulingalirako kuli kotsutsana ndi Mawu, ndiye kulingalirako ndi kolakwika! Mawu ndi olondola, basi momwe Iwo analembedwera! Osayika kutanthauzira kulikonse kwapadera. Mungowanena Iwo momwe Iwo analembedwera, ndi kuwakhulupirira Iwo monga choncho. Mukuona? Mulungu wawasamalira Iwo. Ndizo ndendende basi momwe Iwo akuyenera kukhalira, chotero tiyeni tizingowakhulupirira Iwo mwanjira imeneyo.

²⁷ Tsopano, ndi Mawu, Mawu aliwonse! Aliyense...Mzimu Woyera mwa munthu; chiganizo chirichonse cha Baibulo, Mzimu Woyera mwa inu udzavomereza ndi “ameni,” chifukwa Mzimu Woyera unalemba Baibulo. Ndipo ngati Iye ali mwa inu, Iye

anganene bwanji kuti, “Chabwino, Izo zinali za m’badwo wina, Izo zinali za *ichi*, kapena Izo zinali za *icho*”? Iye anganene bwanji zimenezo ndi kukhala Mzimu Woyera mwa inu? Sangachite zimenezo. Iye akuyenera kunena kuti “ameni” kwa Iwo!

²⁸ Tsopano, monga ine ndinanena tsiku lina, chinthu choyamba chimene Mulungu anawapatsa anthu Ake, kuti chiwamangire linga iwo, chinali Mawu. Ndipo Iye sanasinthepo konse. Iye sangasinthe. Tsopano, tizikhulupiriro sitingagwire ntchito, zipembedzo sizingagwire ntchito, maphunziro sangagwire ntchito, palibe chirichonse cha zinthu izi, chirichonse cha izo chalephera kwathunthu ndipo zidzalephera. Chiripo Chinthu chimodzi chokha chimene chiti chidzachitidwe, ndicho Mawu.

²⁹ Ndipo njira imodzi yokha imene ife tingabwerere mwa Mawu, ndi mwa Magazi. Malo okhawo amene aliyense anayamba wamupembedzapo Mulungu, ankayenera kuti abwere pansu pa Magazi. Palibe kukonzekera kwina kulikonse. Inu simungabwere pansu pa dzina la Methodisti, inu simungabwere pansu pa dzina la Pentekoste, inu simungabwere pansu pa dzina la Katolika. Ilipo mipingo madazeni ya Katolika, yosiyanasiyana, yosiyana wina ndi umzake, Orthodox, ndi Achigriki, ndi Achiroma, ndipo iwo ndi osweka moyipa basi monga Achiprotestanti. Achiprotestanti, Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achilutera, Akatolika, oh, aliwonse, iwo onse ndi mitundu yosiyanasiyana. Ndipo ndi awo apo, mwaona. Koma alipo malo amodzi okha a chiyanjano, ndiwo pansu pa Magazi! Ndipo Magazi ndi Moyo, ndipo izo nthawizonse zidzagwirizana ndi Mawu, nthawizonse ndi Mawu.

³⁰ Tsopano, ife timadziwa kuti moyo umakhala mwa chachimuna, umakhala mmagazi, magazi amoyo. Kupyolera pamenepo thadzi likhoza kuyikira dzira, koma ngati iyo siinakhale ndi mbalame yaimuna, ilo silidzaswa konse. Ndithudi, ilo silachonde. Umo ndi momwe ine ndakhalira, ndapangira maneno achipongwe ambiri, kunena kuti mbalame yaikazi ikhoza kuyikira chisa chodzaza ndi mazira, ndipo iyo ikhoza kukhala yokhulupirika kwa iwo momwe iyo ikufunira kukhalira, iyo ikhoza kuwafungatira iwo, ndi mapiko ake, ndi kuwatembenuza iwo mphindi zingapo zirizonse kuti atsimikize kuti aswa. Ndipo—ndipo iyo ikhoza kukhala ndi njala kwambiri, ndi kusala kudya, pamene iyo ili pa chisa, kuti ikhale yokhulupirika ku mazira amenewo, mpaka iyo nkusauka kwambiri osatha kuwuluka pachisa. Ngati iyo siinakhale ndi mbalame yaimuna, ndipo mazira amenewo nkukhala achonde, iwo akhala mu chisa momwemo ndi kuvunda ngati iyo siikumana ndi yayimuna. Ndizo ndendende.

³¹ Ndipo umo ndi momwe mipingo yathu ikukhalira, yangotengera gulu pansu pa kudzinenera kwa wamba kozizira, kuvina kwina kwachinsinsi kapena kutengeka kwina. Ndipo kodi iwo amachita chiyani? Osawakhulupirira Mawu, mpaka

ife tangokhala ndi chisa chodzaza ndi mazira ovunda. Ndi nthawi yoyeretsa chisa ndi kuyambiranso kachiwiri. Mpaka iwo atalumikizana ndi Mwamuna, Khristu Yesu, ndi kubadwa mwatsopano ndi Mawu. Akatero iwo akuyenera kuswa, chifukwa ndi Moyo.

³² Nthawi ina kale ndinkadya chakudya chamadzulo ndi a—mlaliki wakale wa Methodist, ndipo ndinamva The Agricultural Hour itayatsidwa kuchokera—kuchokera ku Louisville, 4-H Club inali kuyankhula, kuti “Iwo anali ndi makina amene amatha kutulutsa njere ya chimanga monga momwe iwo amalimira mmunda.” Anati, “Iyo ikhoza kupanga mtundu womwewo wa makonifulekisi, mtundu womwewo wa mkate wa chimanga, icho chinali chimanga chomwecho basi. Anachidula icho monga choncho, anachiyika icho pansu pa kuwala, anachitengera icho ku labotare; mtima wake uli pamalo oyenera, ndi chirichonse, ndi kuchuluka komweko kwa chinyezi, kashiamu, potashi, chirichonse chimene chiri mu chimanga chirimo ndendende basi.” Anati, “Ngati mutatenga chodzadza dzanja kuchokera mu thumba la chimene chinalimidwa mmunda, ndi thumba la chimene makinawo amapanga, kapena anapanga, ndi kuchisakaniza icho, inu simungathe nkomwe kudziwa kusiyanitsa kwake ndi diso lanu lachibadwa, kapena mutachidula icho pakati, kapena sayansi iliyonse kuti ikanatha kupeza kusiyanitsako. Njira yokhayo imene inu mungadziwire kusiyanitsa kwake inali kuchikwirira icho.” Mutatero zinganene zimenezo.

³³ Munthu akhoza kuwoneka ngati Mkhristu, iye akhoza kumachita ngati Mkhristu, iye akhoza kumatsanzira Mkhristu. Koma pokhapokha ngati iye ali ndi nyongolosi ya Moyo mmenemo, iye sadzatha kuwuka kachiwiri; akuyenera kukhala ndi nyongolosi ya Moyo imeneyo mmenemo, kukhala ndi Moyo Wamuyaya.

³⁴ Ndipo munthu aliyense amene anaphunzira Chigriki, amadziwa kuti “Muyaya” ameneyo amachokera ku mawu akuti *Zoe*, amene amatanthauza “Moyo wa Mulungu Mwini,” umene unadzakhala gawo la Iye; monga inu muli gawo la atate wanu. Inu mumakhala gawo la Mulungu. Ndipo Moyo Womwe wa Mulungu wagawidwa ndipo wadzayikidwa mwa inu, ndipo Iwo sungafe, chifukwa Iwo ndi Wamuyaya. Chirichonse chimene chinayamba, chidzatha; koma Iye sanachite kuyamba, chotero Iye sangakhoze kutha. Iye ndi Wamuyaya, ndipo ndinu Wamuyaya ndi Iye. Simungakhoze kufa monga Iye sangakhoze kufa, chifukwa inu mumakhala gawo la Iye. Ndinu obadwa mwa Iye. Ameni. Ndikamangopitirira kuyankhula za zimenezo, ndipo sindifika konse ku phunziro ili.

³⁵ Oh, ndine wokondwa kwambiri kukhala Mkhristu! Ine—ine—ine sindingasinthanitse malo ndi aliyense padziko lapansi, osati mapurezidenti, mafumu. Ngati angandipatse

ine dziko lonse, kunena kuti ndikhoza kukhala moyo zaka millions; zikazatha zimenezo ine ndidzafa, zikadzatha zaka millions. Koma tsopano, zaka millions, bwanji, izo sizidzakhala kanthu tsopano, ife tizingopitirira kukhala moyo, popanda imfa. Chotero ndi chabwino kukhala Mkhristu!

³⁶ Ndinali kuyankhula za Abrahamu! Tiyeni tibwerere. Tsopano ife ndi Mbewu ya Abrahamu ngati ife tiri mwa Khristu. Ndiyeno ngati inu muli Mbewu ya Abrahamu, inu muli ndi chikhulupiriro chomwecho chimene Abrahamu anali nacho, chifukwa chinali chikhulupiriro chake chimene ife tikuchikamba. Makamaka mu mpingo tsopano, ndi Mbewu yachifumu ya Abrahamu. Panali mbewu ziwiri za Abrahamu. Imodzi ya izo inali yachirengedwe, Isaki; Imodzi inayo inali Khristu, lonjezo. Chotero kudzera mwa Isaki, Israeli anadalitsidwa; kudzera mwa Khristu, iye anadzakhala atate wa mafuko. Mukuona? Chotero Mbewu yachifumu, iyo ikanakhala yokulirapo motani kuposa mbewu yachibadwa ya Abrahamu. Chotero ngati iwe uli mwa Khristu, iwe umakhala ndi Mbewu yapamwamba, yapamwamba kwa chimene Abrahamu anali, chifukwa iwe wabwera mwa Mbewu yachifumu, Khristu. Ngati muli akufa mwa Khristu, ndiye ndinu ana a Abrahamu, ndipo muli ndi Mbewu ya Abrahamu ndi chikhulupiriro cha Abrahamu. Ndipo chikhulupiriro cha Abrahamu chinali mu Mawu a Mulungu mosalabadira za chimene chinachitika. Iye anazitcha zinthu zimenezo zimene panalibepo ngati kuti zinalipo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Ndi lonjezo bwanji!

³⁷ Tsopano tiyeni tibwerere mmbuyo pang'ono ndipo tikakhazikitse malingaliro athu. Tiyeni tibwerere ku, tisanafike kwa Yehova-Yire, kwa Abrahamu. Tiyeni tibwerere, tigwere mmbuyo pang'ono mu Lemba. Tiyeni tibwerere ku mutu wa 12. Ife tinawerenga apa pa mutu wa 22. Tiyeni tibwerere mmbuyo pa mutu wa 12, pangano limene linapangidwa kwa Abrahamu. Tsopano, pangano, apo panali atatu. . . mapangano awiri.

³⁸ Tsopano, Mulungu amakhala wangwiro mu zitatatu. Ife tikudziwa mawerengero a Mulungu. Ungwiro, mu firii; kupembedza, mu seveni; ndi thwelofu; ndipo forte, ndi yesero; fifite, ndi Chikondwerero; ndi zina zotero, Mulungu mu Ake—manambala Ake. Tsopano, Mulungu amakhala wangwiro mu zitatatu; monga Atate, Mwana, Mzimu Woyera; kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera; ndi zina zotero.

³⁹ Tsopano, apo panali mapangano awiri. Limodzi la iwo linali pangano la Adamu. Mulungu anapanga pangano ndi munthuyo, “Ngati utere, Ine ndidzatero.” Ndipo iye analiswa ilo. Kenako Mulungu anadzapanga pangano ndi Nowa; limenero linali pangano la Nowa, ndipo ilo linadzaswedwa.

⁴⁰ Tsopano Iye akupanga pangano la Abrahamu. Ndipo

pangano la Abrahamu, malingana ndi Genesis mutu wa 12, ilo linaperekedwa mopanda mangawa. Chotero ilo ndi Lamuyaya, chifukwa ilo ndi lopanda mangawa. Osati “Ngati utere, Ine ndidzitere.” Iye anati, “Ine ndatero! Ndachita kale izo.” Osati “Ine *ndidz*achita izo.” “Ine ndachita izo!” Ndizo, oh, izo, izo zimakhazikitsa chikhulupiriro. Mwaona, osati . . . Mulungu ndi wotsimikiza kuti adzapulumutse munthu. Iye anapanga pangano, “Ngati iwe udzitere, Ine ndidzitere,” iye analiswa ilo. Winanso, “Inu mukatere, Ine ndidzitere,” iye analiswa ilo. Munthu sangathe kusunga pangano lake, chotero Mulungu anamupulumutsa munthu ndi chisomo Chake, pansu pa pangano limene liri lopanda mangawa, pangano lopanda mangawa. Oh, mai! Losatha nkomwe, izo zinali zonse za ilo; firii, ungiro. Nowa, Abrahamu, ndipo ine ndikutanthauza . . . Ayi. Adamu, Nowa, ndi Abrahamu. Tsopano, ndi chifukwa chake ife tiri ana a Abrahamu, pangano limenero silingathe, silidzatha, chifukwa ndi lopanda mangawa. Ilo si . . . Si chifukwa chakuti *inu* muchite chinachake; ndi chifukwa chakuti Mulungu anachita chinachake! Osati chifukwa inu munamusankha Mulungu; Mulungu anakusankhani inu! Kodi inu mukhulupirira zimenezo?

⁴¹ Anthu amati, “Oh, M’bale Branham, ine ndinamufunafuna Mulungu ndipo ndinamufunafuna Mulungu!” Ndipo inu simunatero! Ine ndimadana nazo kukuuzani ine zimenezo, koma inu simunatero. Mulungu anakufunanifunani inu. Anali Mulungu akukufunanifunani inu.

⁴² Yesu anati, “Inu simunandisankhe Ine; Ine ndinakusankhani inu. Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye, ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine.” Tsopano, mwaona, izo sizinali. Palibe munthu angadzitamandire mu chirichonse. Ndi Mulungu! Oh, ndi zodabwitsa bwanji kuwona a—chisomo chenicheni cha Mulungu, momwe icho chiliri!

⁴³ Ndipo momwe anthu awutengera Uthenga wa chisomo ndi kuwupanga chochititsa manyazi kuchokera mwa Iwo! Monga mpingo wanga wofunika ndi inu anthu ofunika Achibaptisti, pamene muchisokoneza chisomo monga choncho, inu mwachiika icho kwenikweni mu chisokonezo.

⁴⁴ Winawake ananena kwa ine osati kale kwambiri, anati, “M’bale Branham, tsopano inu mukudziwa inu munali wa Baptisti wabwino.”

Ine ndinati, “Ine ndikumvererabe choncho, koma ndangokwera mmwamba pang’ono.”

⁴⁵ Iye anati, “Chabwino, tsopano taonani,” anati, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye chirungamo. Kodi Abrahamu akanachita zowonjezera zingati

koma kukhulupirira?” Ndipo iye anati, “Pamene tikhulupirira Mulungu, timalandira Mzimu Woyera.”

⁴⁶ Ine ndinati, “Zosiyana bwanji ndi Paulo Woyera! Paulo Woyera ananena, mu Machitidwe 19, ‘Kodi munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene munakhulupirira?’ Osati *pamene* inu munakhulupirira; ‘kuyambira’ pamene inu mwakhulupirira!”

⁴⁷ Iye anati, “Chabwino, Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndizo zonse zimene iye akanachita.”

⁴⁸ Ine ndinati, “Zoono. Koma kenako Mulungu anamupatsa iye dongosolo la mdulidwe, ngati chitsimikiziro chakuti Iye anali atalandira chikhulupiriro chake.”

⁴⁹ Ndipo ngati Iye sanakuduleni inu ndi Mzimu Woyera, Iye sanalandirebe chikhulupiriro chanu. Uko nkulondola. Umenewo ndi mdulidwe wa mtima ndi mzimu. Mulungu amapereka Mzimu Woyera ngati chitsimikiziro kuti Iye walandira chikhulupiriro chanu. Tsopano, ngati inu musiya kukhulupirira, ndi kumangoyenda mozungulira; ndipo kungokhulupirira Mulungu, Mulungu adzadula mtima umenewo. Ndipo izo zimadula kusakhulupirira konse, zimadula dziko ndi kusakhulupirira konse kutali ndi inu; ndipo kenako inu mumaima, Mawu okha. Yesu anati, “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu; ndiye mupemphe chimene inu mukufuna, chidzapatsidwa kwa inu.”

⁵⁰ Limenero ndiro vuto ndi mpingo lero. Uli pansi pa kutengeka, uli pansi pa maphunziro, uli pansi pa kachikhulupiriro. Nzosadabwitsa, iwo wapanikiziridwa pansi! Mukuona? Chotero ife tikusowa mdulidwe, kuti udule chinthu chonsecho. Bwererani kwa Mulungu ndi Mawu Ake, ndipo muwakhulupirire Iwo momwe Iwo analembedwera pamenepo, ndipo osatsutsana nawo Iwo. Mungokhala ndi Iwo. Mulungu anapanga lonjezo, Mulungu amasunga lonjezo Lake. Iye sangachite china chirichonse koma kusunga lonjezo Lake, ndi kukhalabe Mulungu.

⁵¹ Tsopano pangano lopanda mangawa ili. Osati “ngati mudzatero, Ine ndidzatero, koma Ine ndidzatero kenako,” kapena chinachake chonga chimenecho; “Ine ndalipereka kale dzikolo kwa iwe, ndi Mbewu yako ya pambuyo pako!” Amen. Mwaona, anachita kale izo! Ndi ntchito yotsirizika.

⁵² Inu munati, “Kwa Abrahamu Iye anachita izo.” Inde, osati Abrahamu yekha, komanso Mbewu yake ya pambuyo pake.

⁵³ Ndipo ngati ife tiri Mbewu ya Abrahamu, icho ndi chinthu chotsirizidwa. “Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana; iwo amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa; iwo amene Iye wawalungamitsa, Iye wawapatsa kale ulemenero.” Inu mukuchita mantha ndi chiyani? Uko nkulondola. “Ndipo wotsutsakhristu, mmasiku otsiriza,” mogwirizana ndi Chivumbulutso, “ananyenga onse amene ankakhala padziko

lapansi, amene mayina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa ” (kuyambira chitsitsimutso chotsiriza? Ayi) “maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.” Ndi pamene dzina lanu linaikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, pamene Mwanawankhosa anaphedwa. Mulungu anayankhula Mawu; Iwo anali mu kuganiza Kwake, mmalingaliro Ake, Iye anayankhula Mawu ndipo chirichonse chinachitika pa nthawi imeneyo basi. Iyi ndi Mbewu ya Mulungu chabe ikuwonekera, ndizo zonse, Mawu Ake akutsikira pansi. Tsopano, pamene Kuwala kwa Mulungu kuwalira pamenepo, mwamsanga Mbewu imeneyo imazindikira Iko, chifukwa Iyo ndi yobadwa ndi Mulungu. Ndi Mbewu ya Abrahamu, yodziwidwiratu ndi Mulungu. Ndi chifukwa chake Kuwala kumawalira, ndi kuti kukagwire Mbewu imeneyo. Ngati iyo . . .

⁵⁴ Ife takhalapo ndi chitsitsimutso. Yoweri anatero. Ife timakangana kwambiri za mvula yamasika, tinali ndi zochitika zotchedwa “mvula yamasika,” mvula yamasika, mvula yanyundo, mvula yamkati, mvula yakunja. Ine ndinali kuwerenga tsiku lina. Kodi inu mukudziwa chimene *mvula yanyundo* imatanthauza mu mawu Achiheberi? Ine sindingathe kutchula izo pakali pano; ine sindinazilembe izo, izo zalumphha mmalingaliro anga. Koma *mvula yanyundo*, mvula yoyamba, imatanthauza “mvula yophunzitsira.” Mvula yachiwiri ndi Mzimu umene umabwera pa chimene chaphunzitsidwacho, ndipo imabereka chomera. Nchifukwa chiyani ife tinali ndi chitsitsimutso choterocho? Achipentekoste, Abaptisti, mitengo ina yonse inaphuka masamba ake, monga Yesu anati iyo ikanati idzatero. Ndipo kodi ife taswa chiyani? Abaptisti anati iwo “anapeza milioni owonjezera mu ’44.” Tayang’anani pa Akatolika, momwe awonjezekerera. Tayang’anani pa zipembedzo zonse. Tayang’anani pa Pentekoste. Kodi ife tinachita chiyani? Ife tinafesa mbewu zachipembedzo, ife tinakolola zokolola zachipembedzo. Bwanji, mpingo ukuyenera kukhala pa moto kwa Mulungu pakali pano, ngati kunafesedwa mbewu ya Mawu kumbuyo uko, ndipo kungadzakhale zindikiro, zodabwitsa, zozizwitsa, ndipo mpingo umenewo ungasakhale pamodzi, mtima umodzi, mgwirizano umodzi, ndi kumaguba choloza ku Ziyoni, ku Mkwatulo. Uko nkulondola. Kodi ife tinachita chiyani? Ife tinali ndi zoyankhula zaluntha mmalo mwa Mawu. Ife tinali ndi kulingalira motsutsana ndi Mawu, ndi china chirichonse.

⁵⁵ Ife tikuyenera kubwerera ku Mawu. Tiyenera . . . Ife tichita zimenezo! Mulungu anati, “Ine ndidzabwezeretsa, atero Yehova, zaka zonse zimene chimbalinga ndi chirimamine zinadya.” Izo zidzaphuka mu nthawi ya kumadzulo. Padzabwera mmodzi ndi Uthenga, iye adzabwezeretsa mitima, kapena chikhulupiriro cha ana kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate. Iye analonjeza izo mu Malaki 4, kuti Iye akanadzachita izo, kuwabwezeretsanso

iwo kachiwiri.

⁵⁶ Tsopano, ameneyo si Eliya amene anakambidwa mu Baibulo; Yesu anati mu Mateyu 11, “Ngati inu mungalandire icho, Yohane apo anali Eliya amene anali nkudza,” wa Malaki 3. “Taanani, Ine ndituma wa mthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga,” Malaki 3, inu mukazipeza zimenezo.

⁵⁷ Koma kumbukirani, Malaki 4, Uthenga ukubwera, “Tsiku lowopsya la Ambuye lidzafika ndipo lidzawotcha dziko lonse, ndipo olungama adzayenda pa phulusa la oyipa.” Izo sizinachitike pambuyo pa Yohane. Ayi, ngati izo zinali choncho, ndiye Lemba lataya mphamvu Yake, Ilo linanena chinachake chimene sichinali choncho. Ife takhala nazo zaka thuu sauzande chichitikireni zimenezo, dziko silinawotchedwebe chiyambireni, ayi nkomwe. Komanso olungama sanayende pa—paphulusa la oyipa. Koma ife tikuyembekezerabe chinachake chimene chiti chidzatenge Chikhulupiriro, ndi kubwezeretsa chikhulupiriro cha ana kubwerera ku Mtengo wa chipentekoste wapachiyambi umene chimbalanga chinawudya, chimbalanga cha Chiroma, anoni. Zipembedzo zawo zonse ndi tizikhulupiriro zinawudya Iwo. Mulungu anati, “Ine ndidzabwezeretsa Iwo kachiwiri, mmasiku otsiriza.” Ndipo Iwo udzabwezeretsedwa! Mulungu adzatumiza Mzimu Woyera mwanjira yoteroyo, pa Mawu abzalidwa, omwe ati adzabwezeretse. Mawu a Mulungu ndi Mbewu imene wofesa anapita kukayifesa.

⁵⁸ Tsopano, panganolo linaperekedwa mopanda mangawa! Tsopano, Israeli, mbewu yachirengedwe inasinthanitsa zimenezo, ndipo inazitaya izo mu Eksodo 19, pamene iwo anapanga chinthu chopupuluma chimenecho kuti achotse chisomo, ndi kuvomereza lamulo mmalo mwake. Ndi kulakwitsa kopupuluma bwanji kumene Israeli anachita pamenepo!

⁵⁹ Taanani! Mulungu atatha kupanga pangano ndi Abrahamu, chisomo chinali chitapereka kale mneneri wowombola kwa iwo ku Igupto, kuti akachite mawu a Abrahamu. Kumbukirani Mose, pansi pa chitsamba, Mulungu anati, “Ndamva kulira kwa anthu Anga, ndipo Ine ndakumbukira lonjezo Langa.” Pasanakhale lamulo lililonse, chisomo chinapereka izo. Chisomo chinali chitapereka nsembe ya kulakwa kwawo, mwanawankhosa. Chisomo chinali chitapereka pangano, mdulidwe, unali utaperekedwa kale, lamulo lisanabwere. Chisomo chinali chitapereka Lawi la Moto kuti liwatsogolere iwo, kumutsatira mneneri, chitetezero kuti mneneri anali atawauza iwo Choonadi, anali Mawu amene iye ankawakamba. Iwo ankadziwa kuti Mulungu analonjeza izo, ndipo apa panali Lawi la Moto likutsimikizira izo. Ndi chitetezero chowirikiza bwanji! Amen. Chisomo chinali chitachita zimenezo!

⁶⁰ Koma iwo ankafuna chinachake cha iwoeni chimene iwo akanatha kumachichita, kukhala ndi tizikhulupiriro tawo

tawo ndi zipembedzo, ndi chiyandinso-china, kupanga Afarisi, Asaduki, ndi chinachake chimene iwo akanatha kuchita pawokha.

⁶¹ Munthu nthawizonse amayetsa kuti adzipulumutse yekha. Inu simungachite zimenezo! Mulungu anachita kale zimenezo. Inu mukungoyenera kuvomereza izo ndi kuzikhulupirira izo.

⁶² Lawi la Moto kuti liziwatsogolera iwo ndi kuwalondolera iwo, kuwatsogolera iwo pa Njirayo. Mphamvu, chisomo chinali chitapereka Mphamvu kuti imutsutse mdani wawo ndi kuwapanga iwo amfulu. Mphamvu inali itaperekedwa kale. Iwo anawoloka Nyanja Yofiira. Iwo anali atamukantha Farao. Iwo anachita zinthu zonsezi ndi chisomo. Ndipo kenako iwo anasinthanitsa chisomo ndi lamulo, koma izo zinalibe kanthu kochita ndi Mbewu yachifumu ya Abrahamu.

⁶³ Mbewu yachifumu yayetsa kuchita chinthu chomwecho, kubwerera mmbuyo pansu pa mtundu wina wa kachikhulupiriro kmalo motenga chisomo ndi Mawu, ndi kuwakhulupirira Iwo. Anabwerera mmbuyo. Koma padzatulukira Mbewu yachifumu; ife tidzazipeza zimenezo pakapita kanthawi, patsogolo pang'ono.

⁶⁴ Tiyeni tibwerere mmbuyo tsopano ku Genesis 12. Mulungu anamuitana Abrahamu mwa chisomo. Osati chifukwa iye anali munthu wosinthika; iye anali Abrahamu basi, munthu wamba chabe. Osati chifukwa iye anali wansembe kapena wolemekezeka; iye anali mlimi chabe. Iye anabwera kuchokera ku mzinda wa—wa Nsanja Ya Babulo, ndi abambo ake, ndipo anapita ku Kaldeya, Uri wa ku Kaldeya. Ndipo, kumeneko, anali mlimi, mwinamwake ankalima masana ndipo ankalima chakudya chake. Iye anakwatira mlongo wake watheka, Sarah. Ndipo iwo analibe ana, ndipo Abrahamu anali wausinkhu wa zaka sevente-faivi pamene Mulungu anamuitana iye, ndipo Sarah anali wausinkhu wa zaka sikisite-faivi.

⁶⁵ Ndipo Mulungu anamuza Abrahamu pamene Iye anamuitana iye, Iye anati, “Ine ndidzakupanga iwe tate wa mafuko,” ndipo adzamupatsa iye mwana mwa Sarah. Tsopano, iye anali wosabereka. Ndipo iye anali, chabwino, sikisite-faivi, iye anali zaka teni kapena fiftini atadutsa kusintha kwa thupi. Iye anali atakhala ndi iye kuyambira ali ndi pafupifupi usinkhu wa zaka sikisitini kapena eyitini zakubadwa, mlongo wake watheka. Ndipo, iwo, iye anali mwamuna kwa iye zaka zonsezi mpaka iye anafika sevente-faivi, ndipo iye anafika sikisite-faivi, ndipo kenako Mulungu anadzatsika ndipo anati, “Ine ndikupatsa iwe mwana, mwa iye.” Ndipo iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu, koma anakhulupirira ilo!

⁶⁶ Kodi inu mungalingalire mwamuna wachikulire, wa usinkhu wa zaka sevente-faivi zakubadwa, ndi mkazi, sikisite-faivi, akupita kumusi, akunjenjemera, akupita kwa adokotala,

ndikuti, “Adokotala, ndikufuna mukonzekere chipatalacho tspano. Ife tikhoza kukuitanani inu usiku uliwonse, chifukwa, inu mukudziwa, ife tikhala ndi mwana?”

⁶⁷ Dokotalayo angati, “Eya, inde, bwana, ndinu . . . Uh, uh, uh!” Mwamsanga pamene iwo akhala pa foni, angati, “Kulibwino mumutsatire iye, pali chinachake chalakwika.”

⁶⁸ Ndipo aliyense amene amamutenga Mulungu pa lonjezo Lake amaganiziridwa, ndi dziko, “wamisala.” Paulo anati, “Mu njira imene imatchedwa ‘mpatuko,’ ndi momwe ndimapembedzera Mulungu wa makolo athu.” *Mpatuko* ndi “misala,” ife tikudziwa. Ndi zopusa kwa malingaliro achithupithupi. Chikhulupiriro ndi misala kwa aliyense kupatula Mulungu ndi amene ali ndi chikhulupirirocho. Uko nkulondola.

⁶⁹ Koma Mulungu anamulonjeza Abrahamu, ndipo Abrahamu anakhulupirira izo. Iye sanati, “Mulungu, izo zidzakhala motani?” Iye anati, “Chabwino, Mulungu, ine ndikukhulupirira izo.” Ndipo ine ndikukhoza kumuwona iye akupita kunyumba, akuti, “Sarah, tiye tipite kumusi ndipo tikagule mayadi angapo a matewela, ndipo tikagule maphinifolo, ndi kukagula nsapato zina. Tikhala ndi mwana.” Oh, mai!

⁷⁰ Masiku sarte oyambirira anadutsa, kapena masiku twente-eyiti. “Ukumva bwanji, wokondedwa?”

“Palibe kusintha.”

“Mulungu adalitsike, ife tikhala naye, mulimonse!”

“Iwe ukudziwa bwanji?”

“Mulungu ananena chomwecho!”

⁷¹ Ena a ife tikhoza kupemphereredwa usiku umodzi, ndi kukhala mu msonkhano umene Mzimu Woyera ukugwa; ndipo mmawa wotsatira, ngati ife sitiri abwino bwino, abwino, okhazikika, “Ine—ine ndikudwalabe mmimba mwanga pang’ono. Sindingathenso kusintha manja anga.” Iwe, Mbewu ya Abrahamu, usadzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira?

⁷² Chinachake chimabwera mu mpingo, mdierekezi akhoza kufika pakati pa a—gulu la anthu abwino ndi kudzalowa mmenemo ndi kuyamba kukwapula osonkhana amenewo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, ena amati, “Huh, ine ndisiya Chinthu chakale ichi, panalibe kanthu kwa Icho kuyamba ndi kuyamba.” Mbewu ya Abrahamu? Mai, mai! Cholakwika choyamba chaching’ono chimene mdierekezi angakuwonetseni inu, zikatero inu, inu mwathana nacho Icho. Izo zasonyeza kuti simunakhulupirire Icho kuyamba ndi kuyamba.

73 Yesu anati, “Ufumu uli ngati munthu anatenga khoka, ndipo analowa mnyanja ndipo anakaponya mnyanja. Pamene iye amalowa, iye anali ndi chirichonse.” Uko nkulondola.

74 Ndicho chimene—icho ndi chimene chitsitsimutso chimagwira. Mu khokamo muli chiyani? Muli ndi achule, akangaude, akamba, nkhanu, njoka, ndi nsomba. Sipatenga nthawi yaitali mpaka kamba anati, “Chabwino, ano si malo anga,” kubwerera mmatope iye amapita. Kangaude wammadzi wakale anayang’ana pozungulira, ndipo anati, “Uh! Ine sindingakhale ndi masewera amakadi pano.” Chotero mmatope iye amapitanso, monga nkhumba ku matope ake ndi galu ku masanzi ake. Uko nkulondola. Ndipo kenako Mbewu ya Abrahamu? Oh, mai! Chamanyazi choterocho!

Mbewu ya Abrahamu imakhulupirira Mawu a Mulungu!

75 Kukhala kumbuyo uko ndikuti, “Eya, Mulungu adalitsike, ndine wa Chipentekoste!” Ndipo winawake akalalikira chinachake pa Mawu, apo Iwo analembedwa apo pomwe. “Aleluya, ine sindikukhulupirira Zimenezozo. Ayi, bwana.” Mbewu ya Abrahamu? Huh!

76 Tsopano, ngati ziri zamkutu zina, ndithudi, inu simukhulupirira izo. Koma ngati Iwo ali Mawu, Iwo ndi Choonadi! Uko nkulondola. Mbewu ya Abrahamu imagwiritsitsa ku Mawu amenewo osati china chirichonse.

77 Mwezi wina wadutsa. “Sarah, wokonededwa, iwe ukumva bwanji tsopano? Iwe ukudziwa, masiku ena twente eyiti adutsa, iwe ukumva bwanji?”

“Palibe kusintha, wokonededwa.”

78 “Ulemelero kwa Mulungu! Ndi chozizwitsa chachikulu cha miyezi iwiri kuposa momwe chinaliri ngati chinakachitika mwezi watha.”

Chaka chinadutsa. “Kodi nditaye nsapato zazing’onozi?”

79 “Ayi, bwana, iwe uzisunge izo pamenepo. Ife tidzakhala ndi mwana ameneyo!”

“Iwe ukudziwa bwanji kuti ukhala naye iye?”

“Mulungu ananena chomwecho! Izo zikukhazikitsa izo.”

Patapita zaka twente-faivi. “Kodi ukumverera bwanji, Sarah?”

“Palibe kusintha.”

80 “Ulemelero kwa Mulungu! Ndi zaka twente faivi zowonjezera za chozizwitsa tsopano!” Iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akugwiritsitsa ku Mawu a Mulungu; ndi kumatchula zinthu zimene kunalibe, ngati kuti zinalipo. Chifukwa chiyani? Mulungu ananena chomwecho! Oh, mai!

⁸¹ Mbewu ya Abrahamu lero, bwanji, imene ife timaitcha Mbewu ya Abrahamu, ndi yofooka kuposa nsuzi wopangidwa ndi mthunzi wa nkukhu imene yafa ndi njala. Inde, bwana.

⁸² Mulungu amafuna Akhristu okhwima amene amatenga Mawu a Mulungu, kukhala moyo kapena kufa. Ndi chinthu chomwe chomwecho. Amen. “Mulungu ananena chomwecho!” Imeneyo ndi Mbewu ya Abrahamu, yobadwa mwa Mzimu ndi Mawu a Mulungu. Ndicho chimene chimayima.

⁸³ “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita konse.” Ndi zimenezotu. Chimene Mulungu analonjeza, Mulungu ndi wokhoza kuchichita. Mulungu samalephera. Iye sangalephere. Pali chinthu chimodzi chimene Mulungu sangachite, ndipo ndicho kulephera. Iye sangakhoze kulephera, ndicho chinthu chokhacho chimene Iye sangachite. Koma Iye sangalephere. Pamene Mulungu analonjeza icho, ndi Choonadi. Ziri pamenepo kwanthawizonse. Izo zakhazikika kwanthawizonse. Pamene Mulungu ayankhula Mawu, izo zimakhala zokhazikika kale.

⁸⁴ Dziko ili linapangidwa ndi Mawu a Mulungu basi. Iye ankangoti, “Pakhale,” ndipo pamakhala. Amen. Dothi lomweli limene inu mwakhalapo usikuuno, thabwa lomwe mwakhalapolo, si china koma Mawu a Mulungu akuwonetseredwa. Aleluya!

⁸⁵ Ine ndikumamverera mwachipembedzo ndikaganizira za Abrahamu, podziwa kuti ife tikhoza kukhala Mbewu yake, Mbewu ya Abrahamu ndi malonjezo onsewa. Osati kokha kuti azipange izo zotsimikizika, Mulungu anakweza mmwamba dzanja Lake, nalumbira pa Iyemwini, kuti Iye akanadzachita izo. Lumbiriro limakhala, nthawizonse, pangano limatsimikiziridwa ndi lumbiriro, ndipo Mulungu analumbirira pa Iyemwini chifukwa palibe wapamwamba woti angalumbirirepo. Iye analumbirira pa Iyemwini, kuti Iye akanadzachita izo.

⁸⁶ Tsopano chimene dziko, bwanji, chiyani—vuto ndi chiyani ndi ife? Lonjezo loterolo monga ilo! Chikhulupiriro chomangidwa pa chinachake chonga icho, chikhulupiriro chomangidwa! Mawu amene analonjeza zinthu izi mmasiku otsiriza, ndipo apa ife tikuziwona izo zikuchitika patsogolo pathu pomwe, ndipo komabe nkumawerama tikamayenda. Mbewu ya Abrahamu? Oh, mai! Ndikufuna kuti mugwiritsitse kwa izo, “Mbewu ya Abrahamu.”

⁸⁷ Genesis 12, chimene Mulungu ankafuna kwa Abrahamu chinali kulekana kwathunthu.

⁸⁸ Tsopano, lero, iwo akufuna zosakaniza. “Oh, pamene tikumusankha m’busa, iye akuyenera kukhala ndi tsitsi lopiringizika, ndipo azichokera ku Hollywood komwe, inu mukudziwa, ndipo akhoza kunena ‘ah-meni’ mokongola kwambiri, ndipo azivala zovala zapamwamba kwambiri, ndipo

aziwendetsa Cadillac yapamwamba kwambiri, ndi—ndi zina zotero monga choncho, ndipo iye ndi wosakaniza wabwino. Iye azichita *izi*. Ndipo iye azimwa pang’ono kamodzi pakanthawi ndi ife, kuti akhale wochezeka. Iye azibwera ku phwando la makadi la madona okalamba, ndipo iwo azisoka ndi kuluka, ndi kuluka ndi kusoka, ndi kumayankhula za Abiti *Akuti-ndi-akuti*, ndi zina zotero, inu mukudziwa, ndi zonse monga choncho. Ndipo iwo akuyenera kukhala mtundu umenewo wa—wosakaniza.”

⁸⁹ Mulungu anati, “Ndipatulireni Ine Paulo ndi Barnaba!” Amen. Kulekanitsa! “Tulukani pakati pawo ndipo musakhale ogawana nawo zinthu zawo zodetsedwa!” Mulungu amafuna kulekanitsidwa, kuwonongedwa kwathunthu kuchoka ku tchimo. Kulekanitsa! Ndiro limene liri vuto lero, chifukwa chimene ife sitingakhale Mbewu ya Abrahamu, ife sitingadzilekanitse tokha ku nthano ndi tizikhulupiriro, ndi zina zotero, zotchedwa Chikhristu, ku Mawu amoyo. Dzilekanitseni nokha ku kusakhulupirira kwanu, ndipo mukhulupirire Mawu a Mulungu. Mulungu adzadziwonetsera Izo kwa inu. Kulondola.

⁹⁰ Genesis 12, Mulungu anati, “Udzipatule wekha kwa abale ako onse ndi chirichonse chokuzungulira iwe.” Oh, mai, ife timalephera kudzilekanitsa tokha ku kusewera makadi! Huh!

⁹¹ Ine ndinapita ku malo odyera lero, pamene m’bale anabwera mmenemo. Ndinawona wachinyamata wina wopulupudza akulowa mmenemo. Ndipo mkazanga ndipo ine ndimayesera kudya, ndipo ndinaganiza, “Mulungu alemekezeke! Tiyeni tifulumire, wokondedwa, wina asanalowe.” Ndipo wachinyamata wina anadzalowa mmenemo, akudya mosokosa. Ndingachite mantha kukumana ndi mnyamata ameneyo mu mdima. Ndipo iye anayika a—singano yamakina mmenemo ndi, kapena rekodi, ndipo anayamba kusewera zinthu zakale za gwedemula, ndipo—ndipo atayima pamenepo, akupita monga *chonchi*, inu mukudziwa, akudzimenya yekha monga *choncho*. Ine ndinati, “Kalanga ine, chifundo!”

⁹² Meda anati, “Usatero—usapite kumeneko kukalipira bilu imeneyo. Iwe udikirire pomwe pano, undilole ine ndipite ndi iwe.” Iye amachita mantha.

⁹³ Aliyense mmenemo, zinthu zoterezo monga ife tiri nazo lero, fuko la Chikhristu, oh, ndi chinthu chotani! Kudzilekanitsa! Nainte pa handiredi a iwo amayimba mu makwaya, Elvis Presley, ndi Pat Boone, ndi zonsezo, ndi Peabody Ernie, chirichonse chimene iwo amamutcha iye kumeneko. Bwanji, ndi zoyipa kuposa Yudas Iskarioti! Yudas Iskarioti anagulitsa, ndipo anapeza zidutswa sarte za siliva; Elvis anamuposa iye, iye anali ndi ma Cadillac angapo ndi kutchuka kwambiri. Ndipo chifukwa ana aang’ono awa amawona zonse zimene zikuchitika, amati, “Iye ndi wachipembedzo kwambiri.” Ameneyo ndi

mdierekezi! Mwamtheradi! Mulungu samalolera zinthu ngati zimenezo. Ameneyo ndi wochititsa khungu kuno mmasiku otsiriza.

⁹⁴ Bwererani ku Mawu, “Dzilekanitseni nokha ku zinthu zonse zopanda umulungu, ndipo musakhudze chinthu chawo. Ine ndidzakulandirani inu.”

⁹⁵ Uthenga, ife tikuyenera kuwugwira Iwo osavala kanthu mmanja! Osati kuvala magolovesi ena achipembedzo, kumusisita winawake pa nsana, izo zimadzazitsa chisa ndi mazira owola aponso, kumupanga winawake munthu wachigawo, kapena wamkulu, bishopu, kapena chinachake chimzake. Kodi amachita a... Inu mungakhale bwanji ndi chikhulupiriro pamene inu muli ndi ulemu, kulandira ulemu wina kwa mzake? Timayang’ana kwa Mulungu, ndipo Iye yekha! Ulemu umachokera kwa Mulungu. Iye ndiye Mmodziyo. Ife timamulemekeza Iye pogwira Mawu Ake ngati muuni, ndi kumayenda ngati mwamuna kapena mkazi pamaso pa Mulungu. Ndithudi. Kudzilekanitsa kwathunthu!

Genesis 13, Loti anabwerera mmbuyo. Kumbukirani. Iwo anali ndi pang’ono. . .

⁹⁶ Iwo atadzilekanitsa okha, ndi kuwoloka mtsinjewo ndi kukalowa mdzikolo, Mulungu anati, “Abrahamu, Ine ndilipereka lonselo kwa iwe tspano, koma iwe sunandimvere Ine kwathunthu.”

⁹⁷ Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, apo panadza mkangano pang’ono wa olishya, ndi pakati pa oweta ng’ombe awo, ndipo Genesis 13 (chinachitika ndi chiyani?), olishya a Loti ndi olishya a— Abrahamu. Muwoneni Abrahamu, kachitidwe ka ubale, iye anati, “Pasakhale mikangano pakati pathu. Ife ndi abale.” Loti ankaimira mpingo wofunda. Ndipo iye anati, “Yang’ana kunja, panga chisankho. Chirichonse chimene iwe ukufuna, iwe upitirire ndipo ukatenge icho. Iwe ukapita kummawa, ine ndipita kumadzulo, zina zotero. Kapena, iwe ukapita kumadzulo, ine ndipita kummawa. Iwe ukapita kumpoto, ine ndipita kummwera, ndi zina zotero. Iwe upange chisankho chako.” Ndipo Loti anali ali kale ku Igupto ndipo anali ndi chidwi chofuna kutchuka pang’ono, anali ndi ndalama pang’ono mthumba mwake.

⁹⁸ Pamenepo ndi pamene mpingo unapanga kulakwitsa kwake. Ine ndikunena izi ndi ulemu, abale. Mpingo wa Chipentekoste ukanakhala wabwinoko ndi nkhotcho, kunja uko pa ngodya, ndi amuna ndi akazi akachitidwe-kachikale, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, kuposa momwe iwo akanachitira mu akachisi aakulu awa ndi nyumba zosungiramo mitembo zimene iwo akukhalamo lero pansu pa zovunda zonsezi ndi zinthu. Uko nkulondola. Iwo amafuna kuchita monga ena onsewo. Pamenepo ndi pamene tapeza izo. Chifukwa chiyani simunakhale momwe

munakhalira, momwe Mulungu anakuyambirani inu? Chinthu chomwecho chimene inu munkakangana nacho, ndipo inu munatembenuka ndi kuchita chinthu chomwecho.

⁹⁹ Umo ndi momwe Loti ankachitira, anapita ku Igupto ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye anaika maso ake pa Igupto. Ndipo kenako iye anayang'ana uko ndipo iye anawona Sodomu, wapamwamba, akuchita izo mophweka. Ndipo iye anapita kummawa. . . Kumbukirani, anapita kummawa mmalo mopita kumadzulo ndi Abrahamu. Iye anapita kummawa chifukwa inali njira ya moyo wawofuwofu. Iye anapita chakummawa.

¹⁰⁰ Umo ndi momwe mpingo wachitira lero, mwaona, iwo anapita chammbuyo. Monga ine ndinanenera usiku watha, dzuwa limatuluka Kummawa ndipo limakalowa kumadzulo. Ndipo Mwana wa Mulungu anapita Kummawa poyamba, ndipo wapita kumadzulo. Iwo azizimitsa izo, kudutsa zaka thuu sauzande. “Koma padzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo,” mneneri uyu anatero. M'malo motsatira Mwana, iwo amabwerera kumene Mwanayo anali. Lero iwe ukapezeka ukuyankhula chinachake chokhudza machiritso Auzimu, za ulosi, za mphatso naini zauzimu, kapena chinachake; “Tiyeni tibwerere mmbuyo ndipo tikawone chimene Moody ananena, chimene Sankey ananena, chimene Knox ananena, chimene Calvin ananena.” Iwo anakhala mu tsiku limene Mwana ankawalira kumeneko; ife tikupitirira mpaka ku ungwiro! Amen!

¹⁰¹ Wasayansi wa ku France anati, pafupifupi zaka firii handiredede zapitazo, anatsimikizira izo pogudubuza mpira kuzungulira dziko lapansi, iye anati, “Ngati wina angayende liwiro lowopsya la mailosi sarte pa ora, mphamvu yokokera pansu ingawachotse iwo padziko lapansi.” Mwasayansi anatsimikizira izo. Inu mukuganiza kuti sayansi imatchulapo zimenezo? Ayi, bwana! Akuwapangitsa iwo kuyenda pafupifupi mailosi thuu sauzande pa ora, kuyesetsa kuti awapangitse iwo kuti apite patsogolo. Iwo samayang'ana mmbuyo kwa zimenezo.

¹⁰² Koma atumiki, “Timayang'ana mmbuyo ndikuwona chimene Moody ananena, chimene Sankey ananena.” Kumeneko ndi kumene Mwana *anali*. Apa ndi pamene Izo ziri lero! Ziri ku Gombe la Kumadzulo, mu nthawi ya kumadzulo, aleluya, kupereka Kuwala kwa kumadzulo! Osati kubwerera ku kulungamitsidwa kwa Luther kapena kuyeretsedwa kwa Wesley; koma ife tiri pa tsiku lotsiriza, ameni, pamene Kuwala kwa kumadzulo kukuwala, pamene ife tiri pa nthawi yotsiriza. Tsatirani Mwana.

¹⁰³ Koma Loti anabwerera chifukwa kunali kophweka, kwa wofuwofu. Tayang'anani pa Akazi a Loti pamene iwo anabwerera kumbuyo uko. Bwanji, iye akuyenera kuti anali

mfumukazi ya magulu a mu mzinda. Loti anadzakhala meya. Oh, m'bale, iwo anali atazipanga izo, bwanji, ine ndikutanthauza kunena!

¹⁰⁴ Umo ndi momwe anthu awatengera Akazi a Loti lero. Taonani momwe anthu athu akuchitira lero. Tayang'anani pa anthu athu mmatchalitchi, tangoyang'anani pa izo. Tayang'anani pa akazi athu, yang'anani pa iwo lero.

¹⁰⁵ Ine—ine ndinali ku Hollywood lina...kapena ku Los Angeles, posachedwapa, ine ndinkayembekezera M'bale Arganbright kuti abwere. Ndipo apo panayima mtsikana, anabwera pamwamba apo. Ine ndinayang'ana, ndipo ndinadzandima. Ndinamuyang'ana iye. Ine ndinaganiza, "Ndine wa mishonare. Ine ndinawona mliri, ine ndinawona khate, koma ine sindinayambe ndawonapo chirichonse chonga izo." Iye anali ndi limodzi la kumeta phanke, izi, inu mukudziwa, inu mukudziwa, zimene inu mumadzitcha, zinkawoneka ngati phanke, inu mukudziwa, a—Dona Woyamba, eya, munga Yezebeli, munga choncho. Ndipo iye anali ndi zabululu ndi zobiriwira; ndipo mwina ayenera kuti anali mkazi wowoneka bwino; koma zinthu zonsezo pa iye, iye ankawoneka ngati Mkafula wina wa ku Afrika. Ine ndinapita uko, ndimati ndimupempherere mkaziyo. Ine ndinaganiza, "Dona, ngati simukusamala, ine ndimapempherera odwala. Ine sindinayambe ndawonapo chirichonse chonga icho. Ndiwuzeni chimene icho chiri." Ndipo kenako mkazi wina anayamba kuyankhula naye, ndipo iye anali mwanjira yomweyo. Oh, mai!

Oh, inu mukuti, "Ameneyo anali wa Presbateria." Chipentekoste! Ndithudi.

¹⁰⁶ Ndipo Baibulo linati, "Ndi chinthu chopanda ulemu kuti mkazi azimeta tsitsi lake." Iye akachita izo, iye akunyozeza mutu wake. Iye akumunyozeza mngelo, mngelo wa Kuwala. Angelo a Mpingo Asanu Ndi Awiri, amene akubweretsa Kuwala adzakhala ndi Mawu. Zopanda ulemu! Iye akuyenera kukhala ndi tsitsi pamutu pake. Mai, zoterozo! Ndipo izo zinali zolakwika kwa iwo kuti achite zimenezo. Mu—mu Pentekoste yoyamba, izo zimakhala zolakwika. Chinachitika ndi chiyani? Inu munathamanga bwino, chachitika ndi chiyani?

¹⁰⁷ Ndipo ena a akazi athu Achipentekoste amavala madiresi amenewo amene amawoneka ngati chikopa pa kanyimbi, kunja kuno kwinakwake akuyesetsa...Uko nkulondola! Ine sindikunena zimenezo ngati nthabwala. Ano si malo ochitira nthabwala. Pano ndi pa guwa.

¹⁰⁸ Mkazi wina ananena kwa ine usiku wina. Ine ndinawauza iwo momwe ankavalira. Anati, iye anati, "Ine sindimavala zazifupi. Ine—ine—ine ndimavala mathalauza."

109 Ine ndinati, “Izo ndizoyipa kuposa chirichonse. Mulungu anati, ‘Mkazi amene amavala chovala cha mwamuna, ndi chonyansa pamaso pa Mulungu.’” Kulondola!

110 Ndipo ndiloleni ine ndikuuze iwe chinachake, dona, iwe, mkazi wamng’ono, amene umadziveka wekha kunja uko, iwe udzakayankha pa tsiku la chiweruzo chifukwa chochita chigololo.

Iwe ukuti, “Ndine woyera basi ngati kakombo.”

111 Eya, koma Yesu anati, “Aliyense amene ayang’ana pa mkazi kuti amusilire iye, wachita kale chigololo ndi iye mu mtima mwake.” Iwe ukhoza osachita mchitidwewo. “Aliyense amene wamukwiyira m’bale wake popanda chifukwa, wapha kale.” Mwaona, chinthu chokhacho chimene inu mukuyenera kuchita. Ndipo ngati wochimwayo ayang’ana kwa iwe momwe iwe wavalira, zonse kuchitidwa momwe iwe uliri, kubwerera mmbuyo, ndi kukankhira kunja, ndi kukankhira mkati, ndi kuvala mtundu wa zovala zimenezo, ndiye inu mumatuluka. Tsopano mvetserani, zimenezo si nthabwala! Uwu ndi Uthenga! Ndipo iwe umakhala monga choncho, ndipo wochimwa wina amayang’ana pa iwe kuti akusilire iwe. Pa tsiku lachiweruzo, pamene iye azidzayankha chifukwa chochita chigololo, anayambitsa izo ndi ndani? Iwe unatero. Udzayankhira chifukwa unadziwonetsera wekha mwanjira imeneyo.

112 Bwanji, iwe ukuti, “Iwo—iwo sakupanga mtundu wina uliwonse wa zovala.” Iwo akupanga makina osokera, ndipo akugulitsabe nsalu. Palibe chowiringula nkomwe! Ndi chifukwa chakuti mwachoka pa Mawu! Izo si zotchuka. Izo ndi zolimba.

113 Mlaliki wina wotchuka anabwera tsiku lina, ndipo anadzayika manja ake pa ine, anati, “Ine ndiyika manja anga pa inu ndi kuthamangitsa chiwandacho.”

Ine ndinati, “Chiyani?”

114 “Mukuyankhula za akazi amenewo monga choncho.” Anati, “Anthu amakutengani inu ngati mneneri.”

Ndipo anati, ine ndinati, “Ine si mneneri.”

115 Iye anati, “Iwo amakutengani inu monga choncho, M’bale Branham.” Ndipo anati, “Inu mukuyenera kumawaphunzitsa anthu amenewo, akazi amenewo, momwe angapezere madalitso aakulu auzimu. Ndipo muzingowauza iwo za kumeta tsitsi lawo ndi zinthu monga zimenezo. Iwo sangamvetsere kwa izo.”

Ine ndinati, “Ndikudziwa zimenezo.”

Anati, “Bwanji inu osawaphunzitsa iwo zinthu zazikulu?”

116 Ine ndinati, “Ine ndingalalikire bwanji, kuphunzitsa kwa iwo algebra pamene iwo sakudziwa nkomwe ma ABC awo, alibe ngakhale makhalidwe wamba?”

117 Ndipo mwamuna iwe amene ungamawalole akazi ako kumachita monga choncho, ine ndiri ndi maulemu ochepa a inu kukhala munthu wa Chikristu, Mbewu ya Abrahamu. Ameni! Kulibwino ndizisiye izo zokha, ndikupangitsani inu nonse kunyamuka kumapita kwanu. Chabwino. Limodzi la masiku awa inu mudzalephera kupeza chinachake Kumeneko.

118 Inu mukuti, “Izo sizimapanga kusiyana kulikonse.” Izo zinatero kwa Paulo. Izo zinatero kwa Mulungu, mmunda wa Edeni. Baibulo linanena kuti mkazi akuyenera kukhala ndi tsitsi lalitali! Ndipo popanda izo, inu muli pati? Chabwino, inu mukuti, “Izo sizimapanga kusiyana kulikonse.” Baibulo linati izo zimatero! Musalole mdierokezi azikunong’onezani inu, ndi kumakuuzani inu, “Ndi zamakono, ziri bwino.” Izo siziri bwino! Inu munati, “Sindimazidziwa izo poyamba.” Inu mwazidziwa izo tsopano. Mukuona? Fufuzani izo ndipo mupeza ngati ziri zolondola. Ine ndizisiya izo zokha, mwaona. Chabwino.

119 Genesis 13, yamakono, uh-huh; kubwerera kumene Mwana anali, osati kumene Mwana ali; kumene Mwana anali, chonchobe. Mkazi, ndikulingalira, mkazi wa Loti, momwe ankakhalira ndi anthu!

120 Umu ndi momwe ife timakhalira mu gulu la anthu. Umo ndi momwe ife Achipentekoste tinalowera mu zimenezo. Ife timakhala, timakhazikitsa bungwe laling’ono *apa*, ndipo lina laling’ono lotsutsa, lina lotsutsana ndi limzake, ndi kutsutsa *ili*, ndipo iwo amapanga... Inu munatenga chirichonse. Ndizo ndendende kulondola.

121 Kodi Samuele ananena chiyani pamene Israeli ankafuna ku—ankafuna kupanga mfumu, ankafuna Sauli kuti akhale mfumu? Samuele anabwera kwa iwo, ndipo anati, “Kodi ndinatengapo ndalama zanu kuti ndizidyera? Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu kalikonse mu Dzina la Ambuye kupatula chimene chinadzachitika?”

122 Oh, iwo anati, “Ndithudi, iwe ndi mneneri wa Mulungu. Iwe umatiuza ife Choonadi, ndipo zimene umanena zimadzachitika, koma ife tikufuna mfumu, mulimonse.”

123 Ndipo nthawi iliyonse inu mukayamba kusiya zogwiriro, ndi kumaloleza *ichi* ndi *icho*, ndi china chirichonse chibwere monga choncho, inu mwapita mwamakono. Ndipo mpingo uli monga ena onse a iwo lero. Chimene ife tikusowa ndi kusesa mnyumba kwa Chipentekoste! Ndizo kulondola ndendende. Ameni. Ndi chamanyazi kuti wa Baptisti azikuuzani inu zimenezo, sichoncho izo? Koma ndi Choonadi. Kulondola! Ine ndimakhulupirira Baibulo, ndimakhulupirira kuti Mawu a Mulungu ndi olondola. Chabwino.

124 Abrahamu, kenako Abrahamu anatenga... mu ndime ya 14 ya mutu wa 13, Loti atadzilekanitsa yekha, ndipo Abrahamu

anamumvera Mulungu kwathunthu, kenako Mulungu anadza kwa iye. Tsopano Iye ndi wokonzeka kumudalitsa iye.

¹²⁵ Ndipo mpaka mpingo wa Chipentekoste utachoka ku zikhulupiriro zake zonse ndi nthano, ndi kumachita monga dziko ndi kumawoneka ngati dziko, ndi kumayankhula ngati dziko, ndi kumakhala kunyumba Lachitatu usiku kuti muwonere *Ife Timamukonda Susie* mmalo mobwera ku msonkhano wa pemphero, ndi zinthu monga zimenezo, kupereka chakhumi chanu kwa mlaliki wina kunjira kuno pa mtundu wina wa programu ya pa wailesi kumachiseka chinthu chomwecho chimene inu munkaima nacho, kukhala cholondola, ndi mtundu wonse uwu wa zinthu zimene zikuchitidwa mu dzina la pentekoste, ndi chamanyazi!

¹²⁶ Ine ndimawayankhulira Amuna Amalonda Achikhristu, pa dziko lonse. Alipo ambiri a iwo akhala pano tsopano. Kuno usiku wina, kuno pafupifupi chaka chapitacho, zakhala ziripo, ine ndinali ku Jamaica. Ndipo iwo anali ndi otchuka onse a zilumba mmenemo usiku umodzi, ndipo amuna awa akudzuka, akuchitira umboni, “Ulemelero kwa Mulungu! Ine ndinali wochita malonda wamng’ono pa ngodya. Aleluya, ine ndiri ndi ma Cadillac foro tsopano. Ulemelero kwa Mulungu!”

¹²⁷ Ndipo ine ndinabwerera uko ku Flamingo Motel usiku umenewo, ndinayima pamenepo, ine ndinati, “Ndikuchita nanu manyazi inu!” Ine ndinati, “Amuna inu kuno mukuimira Khristu, nkumayesera kumuuzza wamalonda zochulukira zimene inu muli nazo, iye ali ndi zambiri kuposa zomwe muli nazo kapena mudzakhala nazo.” Ndiko kusiyana kochulukira kwathunthu ndi achipentekoste oyambirira. Apentekosite oyambirira ankagulitsa zimene iwo anali nazo, ndipo ankazigawa pakati pa osauka, ndipo ankapita ndi kumakalalikirira Uthenga. Kulondola!

¹²⁸ Woyimba wina wamng’ono wachi Swedish wochokera ku Chicago, ine sindimutchula dzina lake. Iye ndi m’bale wanga wofunika. Iye anaimirira, anati, “M’bale Branham, ngakhale inu. . . Ife timakukhulupirirani inu kuti ndinu mneneri, koma ndikuuzani inu pano, ‘Inu mukulakwitsa.’”

Ine ndinati, “Ndiwuzeni ine ndipati, m’bale.”

¹²⁹ Iye anati, “Chabwino, anthu amenewo ankagulitsa zimene amakhala nazo, ndipo anakaziyika izo pa mapazi a atumwi, ndi kumazigawa izo.” Iye anati, “Two unali mchitidwe woyipitsitsa umene iwo anayamba achitapo.”

¹³⁰ Ine ndinati, “Kodi inu mukutanthauza kundiuza kuti Mzimu Woyera umalakwitsa?”

Ndipo iye anati, “Izo zinali zolakwika. Ine nditsimikizira izo kwa inu.”

Ine ndinati, “Bwanji?”

¹³¹ Anati, “Ndiye pamene chisautso chinayamba, iwo analibe malo oti apiteko. Iwo ankayendayenda, paliponse.”

¹³² “Ndendende mu chifuniro cha Mulungu, kumalalikira Uthenga kulikonse kumene iwo ankapita. Iwo analibe malo oti abwerereko.” Mulungu samapanga kulakwitsa kulikonse. Kulondola! Oh, ndi zosiyana bwanji zimenezo; pentekoste imene inalipo, ndi Pentekoste imene ilipo. Eya, ndi zimenezotu.

¹³³ Abrahamu atadzilekanitsa yekha kwa Loti, basi ndendende zomwe Mulungu anamuuza iye kuti achite. “Kulekanitsa tchimo lililonse limene limatifooketsa mosavuta, kuchotsa chirichonse!” Pamenepo, kenako Mulungu anati, “Abrahamu, tsopano ndiwe wolandira cholowa cha zinthu zonse. Yang’ana kummawa, yang’ana kumadzulo, yang’ana kumpoto, yang’ana kummwera, yenda kudutsa mdzikoli, zonsezo ndi zako!” Ameni.

¹³⁴ Inu mulekanitse chinthu chanucho, inueni ku tchimo, kusakhulupirira. Pali tchimo limodzi lokha, ndipo ndiro kusakhulupirira. Kuchita chigololo si tchimo, kumwa mowa si tchimo, kunena mabodza si tchimo; izo ndi zotsatira za kusakhulupirira. Ngati mukanamakhulupirira, inu sibwenzi mukuchita zinthu zimenezo. Ndithudi. Yesu ananena mu Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya,” Zoe imeneyo, Mzimu Woyera, chifukwa iye anakhulupirira. Molondola. Tsopano, mpaka inu mutalandira Iwo, ndinu odzipangitsa-kukhulupirira, amene ali mu gulu limenero. Koma pamene iwo akhulupirira kwenikweni, kudzilekanitsa okha, ndiye pamene mudzilekanitsa nokha ku kusakhulupirira kwanu konse, ndi kumukhulupirira Mulungu, kumayenda uko mosamalitsa, kumanyamula Malamulo, kumachita chirichonse chimene chiri cholondola, ndiye Mulungu adzati, “Lonjezo lililonse la m’Bukhu ndi lanu.” Ameni. “Zonse ndi zanu! Tembenukani muchoke kwa Ilo, kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso, zonsezo ndi zanu!” Ameni. “Ngati inu mudzakhala mwa Ine ndi Mawu Anga mwa inu, inu mukhoza kudzapempha chimene inu mukufuna, icho chidzakhhalapo.” Chiyani? Inu mukuyenera kudzilekanitsa nokha, choyamba, ku kusakhulupirira kwanu.

Inu mukuti, “M’bale Branham, inu mukuzipangitsa izo mwapafupi kwambiri.”

¹³⁵ Yesu anati, “Mmasiku a Nowa panali eyiti amene anapulumutsidwa. Monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu Kudza kwa Mwana wa munthu.”

¹³⁶ “Ndi angati amenewo, M’bale Branham?” Iwo akhoza kukhala eyiti sauzande, mwina eyiti milioni, ine sindikudziwa chimene icho chiri. Koma zidzakhala mwa ochepa. Mmodzi pa

handirede sauzande iliyonse, kapena chinachake chonga icho, ine ndikhoza kutero. Chabwino.

¹³⁷ Chikhulupiriro chammaganizo, chikhulupiriro chamalingaliro, chopanda zokuchitikira za kubadwanso mwatsopano, zotengeka, kachikhulupiriro kachipembedzo! Ngati Mzimu Woyera weniweni uli mmenemo, Iwo udzatsimikizira Mawu amenewo; ndipo Mawu amenewo adzakhala ndendende basi monga Iwo unati Iwo akanati adzakhale, chifukwa Iwo ndi Mzimu womwewo umene unayankhula Izo, ukuyankhula Izo kupyolera mwa inu. Iwo ukuyenera kukhala moyo. Ndithudi, izo ziri. Osati inu amene mukuyankhula, koma Atate amene ali mwa inu, Iye ndi Amene amayankhula. Chabwino.

Abrahamu, wolandira zinthu zonse.

¹³⁸ Ine, pamene ndinadzazidwa ndi Mzimu Woyera monga inu anthu munachitira, ine ndimakonda kudutsamo, ndipo, monga sitolo yayikulu, chirichonse mmenemo ndi changa. Ndine wolandira gawo lililonse la izo. Ndipo ngati ndinalandira sitolo yayikulu, ine—ine ndikufuna kudziwa zimene ndiri nazo. Pamene ndinadzakhala Mkhristu, ndinkafuna kudziwa zomwe ndinali nazo. Chotero ngati ine ndinali ndi sitolo yayikulu, ine ndingadutse, ndi kukoka chitseko ndi kuwona zimene ziri mmenemo, ndi kuyang'ana cha *apa* ndi kuwona zomwe ziri mmenemo; chinachake chikuwoneka kuti chiri pamwamba pang'ono pamenepo, ine ndingapeze makwerero ndi kukwera kuti ndikafikire kwa icho. Ndingafufuze chimene icho chinali. Chinachake chikuwoneka kuti sindingachifikire apa, ine ndingagwade pa maondo anga ndi kuyamba kupemphera mpaka ine nditakwera kwa icho. Icho ndi changa! Mulungu analonjeza izo. Machiritso auzimu, Mphamvu ya Mulungu, zozizwitsa zonsezi ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, Iye analonjeza izo.

¹³⁹ Mukuti, “M’bale Branham, kodi zinthu izi zimagwira bwanji ntchito?” Mwa lonjezo la Mulungu. Ameni.

¹⁴⁰ Mbewu ya Abrahamu! Ulemelero! Ndikumverera bwino. Ndikhoza kuwoneka wamisala ndi kumachita mwamisala, koma ingondisiyani ine ndekha. Ine ndimamverera bwino mwanjira iyi kuposa momwe ndimamverera mwanjira inayo. Mukuona?

¹⁴¹ Mutu wa 14, ife tikupita kwa Abrahamu, tsopano ife tikupeza pa mutu wa 14 chimene chinachitika. Mafumu anabwera kuchokera ku madera osiyanasiyana a dzikolo, ndipo anapanga chitaganya ndi mafumu a Sodomu, ndipo analowa mmenemo ndipo anakalanda Sodomu, anakamutenga Loti; M’bale wake wa Abrahamu mwa Ambuye, anakamutulutsako iye, m’bale wake wofunda wachipembedzo, ndipo anapita naye iye. Tsopano, kumbukirani, Mulungu anali atangomuza Abrahamu kuti chirichonse mu dzikolo chinali chake.

142 “Ndipo ofatsa adzalandira dziko lapansi.” Mukuti ndife amisala? Tidzatenga dziko lapansi, zimene ziri padziko lapansi! Ndithudi, ndife olandira a ilo.

143 Yang’anani kwa Satana, anati kwa Yesu, “Ngati Iwe ugwada pansu ndi kundipembedza ine, ine ndikupatsa Iwe dziko ili.” Maufumu onse akulamulidwa ndi mdierekezi, uliwonse wa iwo. Yesu ananena chomwecho. Baibulo limayankhula izo. Fuku lililonse ndi ufumu uliwonse zikulamulidwa ndi mdierekezi. Ndipo Satana anati, “Ine ndi mwini wa izi. Izo ndi zanga. Ine ndidzapereka izo kwa Iwe ngati Iwe udzandipembedza ine.”

144 Yesu ankadziwa kuti Iye anali Wolowa kwa iwo mu Zakachikwi, chotero Iye anati, “Pita kumbuyo Kwanga, Satana.” Iye ankadziwa kuti Iye anali Wolowa wa izo.

145 Ndipo lero iwo amakamba za anthu openga akupembedza Ambuye ndi kubadwa mwatsopano. Iwo amawopa za “kubadwa mwatsopano.” Iwo basi samalikonda lingaliro limenero, ndipo iwo analoweza mmalo chinachake mwa ilo. Mmodzi wa iwo walowetsamo kugwirana chanza mmalo mwake; winayo, kuwaza kukonkha pang’ono kwa madzi; mmodzi winayo, kutulutsa lirime lake kunjira ndi kutenga chidutswa cha mkate; mmodzi winayo, amavina pansu. Ndi Kubadwa! Monga ine ndinanena usiku wina, “Kubadwa ndi nyansi, sindikusamala kumene zikuchitikira. Ngati izo zikuchitikira mu khola la nkumba kapena chipinda chachipatala, ndi kubadwa, ndi nyansi.” Ndipo chomwechonso ndi Kubadwa kwatsopano, Iko kumakung’amba iwe, koma kuchokera mu nyansi imeneyo mumabwera Moyo watsopano. Amen. Inde.

146 Abrahamu ankadziwa kuti chirichonse chinali chake, chotero pamene Loti analowa, iye anati, “Tsopano dikirani miniti.” Loti anatulutsidwa ndi manja ankanza a mdani. Iye anati, “Ameneyo ndi m’bale wanga, ndipo ndimutsatira iye.” Tsopano kumbukirani, apo panali pafupifupi mafumu seveni kapena eyiti kumeneko amene anabwera pamodzi, ndipo anabwera kumeneko ndi kudzatenga chirichonse ndipo anasesa ndi icho. Ndipo pamene iwo anatuluka, Abrahamu anatenga antchito ake ndipo anamutsatira iye, kuti akamubweretse m’bale wake wotayikayo. Ameneyo ndiye Mkhristu weniweni, anamutsatira m’bale wake wotayika! Kodi iye anachita chiyani pamene anakamupeza iye? Anawapha mafumuwo; ndipo anabwerera, akumubweretsa m’bale wake, itatha nkondoyo.

147 Taonani, apo panali Mfumu imodzi imene inatuluka kukakomana naye iye, akubwerera, Melkizedeki. Melkizedeki, kodi Iye anali chiyani? Iye analibe abambo, Iye analibe amayi. Iye sanabadwe konse, Iye samafa konse. Wopanda abambo, wopanda amayi, wopanda chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo. (Iye sanali Mwana wa Mulungu; chifukwa Iye anali ndi Atate ndi amayi, awiri onse anabadwa ndipo

anafa, ndipo anawuka kachiwiri.) Koma Munthu uyu analibe abambo kapena amayi, Iye ndi Mulungu! Ndithudi, Ndi Chinthu chokhacho chimene chiri Chamuyaya.

¹⁴⁸ Ndipo Iye anakomana ndi Abrahamu nkondo itatha, kuwonetsera izo kwa Mbewu ya Abrahamu; titatsatira m'bale wathu wakugwa, ndipo nkondoyo ikadzatha. Kodi Melkizedeki anapereka chiyani? Vinyo ndi mkate, mgonero. Amen. Pamene nkondo idzatha, m'bale! Anabwereranso, akumubweretsa m'bale wake wotayika kubwerera kunyumba, kumubwezeretsanso iye. Ndipo pamene nkondoyo inatha, Melkizedeki anakomana naye iye ndipo anamupatsa iye mgonero. Yesu anati, "Ine sindidzadya kapena kumwa chipatso cha mpesa panonso kufikira Ine ndidzadye icho mwatsopano ndi inu mu Ufumu wa Atate Anga." Inde, bwana. Tsopano nkondo inali itatha, Abrahamu anali atabwerera, mutu wa 14; ndipo Mgonjetsi anakumana naye, pamene iye ankalowa ndi Mgonjetsi.

¹⁴⁹ Genesis 15 tsopano, ife tisanatseke, chifukwa ndi nthawi yotseka tsopano. Tamvetserani chinthu chimodzi chinanso ife tisanapite.

¹⁵⁰ Ndipo ine ndikuyenera kuti ndidzatenge izi mawa usiku kachiwiri, chifukwa ine sindinafike pa phunziro langa, ine ndifikabe pa malo anga, pa *Yehova-Yire*. Ine ndikufuna ndizitengere izi panso apo, ngati Ambuye alola.

¹⁵¹ Tsopano pa mutu wa 15, ine ndiri nazo apa kuti pangano linatsimikiziridwa kwa Abrahamu, chitsimikiziro cha pangano. Mwa kuyankhula kwina, ndi pamene Mulungu analumbira, ndipo pamene Mulungu anapanga lonjezo ndi kutsimikizira lonjezo kwa Abrahamu. Pa mutu wa 15, ife tikupeza kuti, kutsimikizira kwa lumbiro limene Mulungu ananena.

¹⁵² Abrahamu anati kwa Mulungu, "Wolowa nyumba yanga akanali Elieza wa ku Damasiko."

¹⁵³ Ndipo Iye anati kwa iye, "Koma ameneyo si wolowa mmalo wako, pakuti ndi mmodzi wa mmimba mwako ndiye wolowa wako." Ndipo Iye anamulonjeza iye.

Anati, "Ndidzadziwa bwanji izi?"

¹⁵⁴ Oh, tsopano, abale, apa pali chinachake chimene chidzakudzutseni inu! Muoneni Iye. Iye anati, "Pita ukanditengere Ine mbuzi yaikazi ya zaka z tatu, ng'ombe yaikazi, ya zaka z tatu, ndi nkhusa yamphongo ya zaka z tatu." Ndipo Abrahamu anatenga izo, ndi nkhusa ziwiri. . . nkhusa ndi njiwa.

¹⁵⁵ Tsopano, nkhusa ndi njiwa ziri ndi choyimira; nyama za zaka z tatu izi, ndipo panali z tatu za izo. Tsopano Iye apanga pangano, atsimikizira pangano. Tsopano mvetserani

mwatcheru, musaphonye izi. Ndipo kenako ife tidzazitenga mawa usiku pamene Iye akukumana ndi iye kuno kachiwiri, Ambuye akalola. Penyani.

¹⁵⁶ Tsopano Iye anati, “Nditengere Ine a—ng’ombe yaikazi ya zaka zitatu, mbuzi yaikazi ya zaka zitatu, ndi nkhoa yamphongo ya zaka zitatu, ndi njiwa, ndi nkunda.”

¹⁵⁷ Ndipo Abrahamu anapita ndipo anakatenga ziwetozo, ndipo anazidula pakati ndi kuziika izo, chidutswa pa chidutswa; koma nkunda ndi njiwa, iye sanalekanitse nkunda ndi njiwa. Nkhunda ndi njiwa ndi banja limodzi. Chotero izo zinkaimira machiritso Auzimu, chimene mu mapangano onse awiri ndi mwa chikhulupiriro, mwaona, kuti iwo amachiritsidwa; mmodzi kwa mzake, winanso. Ngati pangano lakale linali ndi machiritso Auzimu mmenemo, ndi mochuluka bwanji momwe ili liri nawo Amodzi! Mwaona, ngati nsembe yakale inali ndi machiritso, nanga bwanji Iyi imene ili yabwinoko kwambiri! Mukuona?

¹⁵⁸ Tsopano, koma zindikirani chimene iye anachita apa. Iye ankatenga ziweto zitatu izi ndi kuzidula izo pakati, ndi kuziika izo, chidutswa ndi chidutswa. Ndipo kenako Abrahamu anabwerera. Tsopano, imeneyo inali nsembe. Ndipo iye ankayang’anira mpaka dzuwa lilowe. Ndipo mbalame zimatsika kuchokera mu mlengalenga, pa nsembe ya Abrahamu, akhungubwe. Ndipo Abrahamu ankawathamangitsira iwo panja, amawathamangitsira iwo kutali.

¹⁵⁹ Kodi ndi choyimira chiyani ichi? Mbewu ya Abrahamu mu tsiku lotsiriza, ikutulutsa ziwanda kuzichotsa pa Nsembe, kuzithamangitsa kuzichotsa pa Nsembe. Mulungu analonjeza izo, Nsembe, Khristu, yemweyo dzulo, lero, kwanthawizonse, ndi mizimu yonse yosakhulupirira iyo ikuyesera kuti ilikhwire Iyo. Munthu wa Mulungu, Mbewu ya Abrahamu, wayima pamenepo akutulutsa ziwanda, kuzichotsa kwa Iyo! Kutsimikizira pangano tsopano, chitsimikiziro, kusonyeza kuti Mbewu ya Abrahamu mu...Ine ndikutanthauza Mbewu yachifumu yokhulupirika. Kumbukirani, mbewu yachibadwa inalephera, chifukwa iyo inavomereza lamulo mmalo mwa Mawu a chisomo. Ndipo chomwechonso iyo yatero mu uku “kuzungulira,” mwa Amitundu mu tsiku lotsiriza. Koma ilipo Mbewu, Mbewu yachifumu yokhala ndi Mawu, yaima moona, kutulutsa ziwanda, kumachita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa, kuchotsa kusakhulupirira konse ku Mawu, kusunga Nsembe kukhala yoyera, kusunga Mawu kukhala oyera, kuwasunga Iwo molemekeza; osayika chirichonse ndi Iwo, kuwonjezera chirichonse kwa Iwo; kumangoyingitsira izo kutali, kuyima mwatcheru, osaloleza chirichonse chikhudze Iwo.

¹⁶⁰ Tsopano zindikirani, apo panadza tulo tatikulu pa Abrahamu, imfa. Ndipo atagona tulo tofa nato, iye anawona ng’anjo yamoto, imene ili gehena, yofuka, imene wochimwa

aliyense akuyenera kupitako. Koma kusanapite Kuwala kwakung'ono koyera. Penyani Kuwala kwakung'ono koyera kuja, kumapita pakati ndi kudzalekanitsa nsembe izi, kumapita pakati pa izo, Mulungu akutsimikizira chimene kupyolera mu Mbewu ya Abrahamu Iye akanadzachita.

¹⁶¹ Tsopano, Ayuda nthawizonse ankakhulupirira kuti Mulungu anali Mmodzi. Ndipo Mulungu ndi Mmodzi. Koma Iye ankawonetsera apa, mwa nsembe zitatu zoyera izi, kuti utatu wa Mulungu udzaimiridwa mwa Mmodzi mu Umulungu mwathupi.

¹⁶² Tsopano zindikirani mu akale—masiku akale, mmasiku akale, pamene pangano likupangidwa, umu ndi momwe iwo ankachitira izo. Monga, ife tinabwera ndipo tinapha nyama, tinagawa nyamayo pakati, ndipo tinayima pakati pa nyamayo, ndipo pamenepo tinalemba pangano. Tsopano ku China . . .

¹⁶³ Momwe ku Japan, pamene iwo akupanga pangano, iwo amatenga mchere ndipo amayima ndi kupanga lonjezo lawo, ndipo amaponyerana mchere pa wina ndi mzake. Umo ndi momwe ku Japan, amapangira pangano, amaponyerana mchere. Mchere ndi wokometsa, mwaona. Ndipo iwo amaponya mchere pa wina ndi mzake, ndiro a—ndiro a—pangano.

¹⁶⁴ Tsopano mu Amerika, momwe ife timapangira pangano, ife timapita kunja ndi kukapeza chakudya kuti tidye, ndi kugwirana chanza, “Ndipatse dzanja lako, mnyamata. Kodi tagwirizana?” “Tagwirizana izo!” Ndiro pangano.

¹⁶⁵ Koma mu nthawi zakale, mu nthawi ya Abrahamu, momwe iwo ankapangira pangano kunali kupha nsembe, ndipo amayima pakati pa nsembe iyi; ndipo kenako, pamene iwo atero, iwo ankalemba pangano pa chidutswa cha chikopa cha mwanawankhosa, kenako ankang'amba icho. [M'bale Branham akung'amba kachidutswa ka pepala kuti awonetsera—Mkonzi]. Mmodzi ankatenga chidutswa chimodzi, ndipo mmodzi ankatenga chinacho. Tsopano pamene pangano ili litsimikiziridwa ndi kubweretsedwa pamodzi, panalibe mmodzi akanakhoza kutsanzira izo. Mwaona, izo zimayenera kulumikizana, chilembo ndi chilembo, chimodzimodzi basi momwe izo zimakhallira. Zimenezo zinkasonyezera kuti mwiniwake wa chidutswa ichi ali ndi gawo, ili ndi pangano lomwelo, kuti iwo akuyenera kubwera pamodzi ndi kulumikizana chimodzimodzi basi.

¹⁶⁶ Ndipo Mulungu ankawonetsera pamenepo kwa Abrahamu, kuti kupyolera mu Mbewu yake, kuti Mulungu Mwiniwake akanadzakhala thupi ndipo kenako adzayenera adzalekanitsidwe pa Kalvare; kumene Khristu, pokhala Mulungu pa dziko lapansi, Iye analekanitsidwa. Mulungu anamung'amba Iye pakati, Mbewu yachifumu ya Abrahamu, ndipo anachotsa Moyo mwa Iye; ndipo anawukitsa Thupilo,

kuti likakhale pa Mpandowachifumu Wake Kumwamba; ndipo anatuzanso Mzimu wa Iye pa Mpingo, kuti Mpingo ukuyenera kukhala ndi womwewo—Mzimu womwewo umene unali mwa Khristu kuti apangitse izo kubwera pamodzi, kumupanga Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Kutsimikizira kwa pangano, Mulungu kutsimikizira pangano. Mulungu kulekanitsa, kuwung'amba Moyo kuwuchotsa mwa Khristu, Mwana Wake, kuwuchotsa Mzimu mwa Iye; pamene Iye ankazidula nyama zimenezi pawiri, nkuyima pakati pa nyamazo. Kuwala, Mulungu Mwiniwake, ankapita pakati pawo, kuwonetsera kuti Iye walilekanitsa Thupilo: Mbewu, Mbewu yachifumu; ndipo watenga Mzimu ndipo wawutumizanso Iwo pa Mpingo. Ndipo Mpingo wa lero umene umapita kukakomana ndi Khristu, ukuyenera kukhala ndi Mzimu womwewo umene Iye anali nawo, chifukwa izo zikuyenera kukhala Chilemba ndi Chilemba, Mawu ndi Mawu. Ndipo Iye ndi Mawu! Yesu anati, “Iye” (puronauni ya umwini) “amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Kutsimikizira pangano, Moyo umene uli mwa Khristu udzakhala mu Mpingo, Mbewu yachifumu ya Abrahamu.

¹⁶⁷ Mphindi, abale, pa Pentekoste. Pamene iwo anali mchipinda chapamwamba... Ngati inu munayamba mwakhalapo kumeneko ndi kuwona chithunzi chenichenicho, momwe icho chinajambulidwira, iwo ankazungulira masitepe kunja ndi kukwera kupita mchipinda chapamwamba. Iwo anakhala ndi makandulo aang'ono a mafuta a azitona akuyaka. Iwo anakhala kumeneko kwa masiku teni ndi usiku, zitseko zonse zitatsokedwa. “Ndipo mwadzidzidzi panabwera phokoso kuchokera Kumwamba ngati mphepo ya nkokomo yamphamvu, Iyo inadzaza nyumba yonseyo kumene iwo anakhala. Malirime ogawanika ngati moto, malirime ogawika a moto, anadzakhala pa aliyense wa iwo. Onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera, anathamangira panja, akuyankhula mu zinenero zina.”

¹⁶⁸ Zindikirani, Moto wogawanika uwu unali chiyani? Unali Lawi la Moto, Mzimu Woyera, Mulungu, Mngelo amene anawatsogolera iwo mchipululu, Iye amene anawonetseredwa pamaso pawo. Mulungu anali atadzilekanitsa Yekha ndipo anadzigananza Yekha pakati pa anthu, Mzimu Woyera, ndipo pamodzi ife ndi Mpingo wa Mulungu wamoyo. Pangano! “Abrahamu ndi Mbewu yake pambuyo pake, Mbewu yachifumu.” Moyo womwewo umene unali mwa Khristu, mu Mpingo, ukuchita ntchito zomwezo zimene Khristu ankazichita. Amen. Ndi chinthu chodabwitsa bwanji, abwenzi!

¹⁶⁹ Yakwana nthawi, ine ndikuyenera kuti nditseke izi. Inde, ine ndichedwa kwambiri. Ine ndi... Kodi zingakhale bwino ngati ndingazitenge izi mawa usiku pomwe pano? Ine ndikufuna kufika ku *Yehova-Yire* moyipa kwambiri. Koma ine ndikufuna inu muwone chimene icho chiri, kuti chinthu chodzinerera

kukhala Mkhristu, abale, ndi nthawi imene mpingo upeze a . . . Ngati Mulungu anapanga malonjezo awa, iwo ndi owona. Iwo akuyenera kukwaniritsidwa.

¹⁷⁰ Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi yokha. Izi ndi zokandapala komanso zolimba. Izo ndi zodula. Ine sindimakonda kuchita zimenezo. Mtumiki uyu anati kwa ine, iye anati, “M’bale Branham, chifukwa chiyani *chakuti-ndi-chakuti*, inu mukuchita zimenezo?”

¹⁷¹ Ine ndinati, “Ndilibe maprogramu a pa kanema oti azithandizidwa, wailesi. Ine ndimangopita monga chonchi, kumene ine ndingathe kupita kulikonse.” Ine ndinati, “Ndani ati akawawuze iwo? Pakuyenera kukhala liwu penapake lizikanena izo.”

¹⁷² Tsopano Mulungu ali pano, abwenzi. Ndipo ngati inu mwadzitcha nokha Mbewu ya Abrahamu, ndipo mukuganiza kuti inu . . . Tsopano musatero . . . Mvetserani, ndi moyo wanu, mzanga. Ndi moyo wanu. Musatengerepo mwayi uliwonse pamenepo, chifukwa usikuuno ukhoza kukhala nthawi yotsiriza kuti mupeze mwayi. Ngati inu mukuchita manyazi ndi moyo wanu, kudzitcha nokha mwana wa Mulungu, ndi kumakhala momwe inu mwakhalira moyo; ndipo inu mukukhulupirira kuti Mawu a Mulungu ndi owona, ndipo inu mukulakwitsa, ine ndikufuna inu mungopemphera kwa mphindi, mumupemphe Mulungu kuti afufuze moyo wanu. Mungopemphera basi.

¹⁷³ Atate Akumwamba, uwu ukhoza kukhala usiku womaliza kwa ambiri a ife. Ife tikuganiza, mausiku angapo apitawo mu Los Angeles, mzimayi wachikulire wa usinkhu wa zaka sevente zakubadwa atakhala pamenepo, ndipo iye anayenda mpaka ku guwa ndipo anapereka moyo wake kwa Khristu. Usiku umenewo iye anamwalira ali pa bedi. Chisomo cha Mulungu, ora lotsiriza lija. Atakhala zaka zonsezo osamudziwa Iye, kenako anamuyitana iye pa ora lomaliza. Chisomo chodabwitsa.

¹⁷⁴ Atate Mulungu, yankhulani kwa mitima pano usikuuno. Mukudziwa cholinga cha izi. Inu mukudziwa, Atate, ndi—ikuyenera kufika nthawi imene chinachake chikuyenera kuchitika. Ife—ife tikuwona chikhalidwecho, ndi momwe zikuyipirayipira nthawi zonse. Ndipo ife tikuzindikira kuti m’badwo wa mpingo wa Chipentekoste, mmasiku otsiriza, ndi M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, wokhawo umene Khristu anayikidwa kunjwa kwa mpingo, atayima, akugogoda akuyesetsa kuti abwerere mkati. O Mulungu, tichitireni chifundo.

¹⁷⁵ Ndipo pamene ine ndimawazazira alongo athu usikuuno, Ambuye, kuwadziwitsa iwo kuti kumbuyo uko pachiyambi, pamene izo zinkayamba, anali Eva. Ndipo ndi izi apa kachiwiri. Uthenga unabwera ndi Mawu, ndi momwe iye anachitira zimene iye anachita (ndipo taonani lero) mwa kulingalira; tayang’anani

pa amayi ake, zimene iwo ankaganiza kuti zinali zosiyana, Baibulo lomwelo.

¹⁷⁶ Mulungu, abale athu, monga ine ndimayenera kuyankhula nawo molimba, Ambuye. Ndine wakhama, ine—ine—ine ndimawakonda iwo. Inu mukudziwa ine ndimatero, Ambuye. Ine—ine—ine ndawayikira iwo zaka sarte-wani pano, ndipo Inu mwatsimikizira Mawu Anu, ndi china chirichonse. Ambuye, ine sindikudziwa chinanso choti ndichite. Koma pamene ine ndiwuwona mpingo umene ine ndimawukonda, mpingo wa Chipentekoste, umene unaima kumbuyo kwanga ndi kundithandizira ine; Mulungu, ndi chikondi cha Chikhristu chimene chimakupangitsani Inu kuchotsa choyipa kwa icho. Ndi chikondi chimene chimakupangitsani Inu kuchita zimenezo, Atate. Inu mukudziwa izo ziri. Ndipo ine ndikuyesetsa kuwawuza anthu, “Musayesere kupita kunja uko, kumakachita zinthu izi.” A—zogwirira zasiyidwa, ndipo ife taswa kupyolera mu tizikhulupiriro tathu tosiyanasiyana ndi zinthu zimene ife tazibweretsa mu mpingo, ndi kuchoka ku masiku a zozizwitsa, kuchoka ku machiritso Auzimu, kuchoka ku—momwe anthu akuyenera kuchitira ndi kuvala.

¹⁷⁷ Ndipo Inu munapanga pangano ndi Adamu, ndi limodzi ndi Eva; Inu munayika pangano losiyana, ndi losiyana pamodzi, ndipo munati zinali zolakwika kuti mkazi azichita monga mwamuna. Iye adzakhala wachikazi. Iye akuyenera kukhala wachikazi osati wachimuna. Ndipo lero iye akuyesera kuti akhale wachimuna; mwamuna, wachikazi.

¹⁷⁸ Ambuye, ndipo—ndipo izi pomwe pano mmasiku otsiriza, pomwe pano pa Gombe la Kumadzulo, pomwe pano ku mapeto a chitukuko, ife timawapeza akazi akuchita ndendende chivundi monga iwo ankachitira poyamba. Ndipo ndi izi apa, zafika pakati pa alongo athu. O Mulungu, izo basi zimangoswa mtima wanga, Ambuye. Ndipo ine ndikudziwa ngati izo zimandipangitsa ine (wochimwa) kumverera mwanjira imeneyo, kodi izo zimachita chiyani kwa Inu, kuwona momwe izo zakhalira mulungu wamkazi. Ndipo kukongola kwapamwamba kwa Hollywood uku kwa tchimo! Ndipo izo zinali zolakwika kuti iwo azipita ku ziwonetsero za zithunzi, kenako mdierekezi anaziponyera izo mnyumba mwawo momwe, ndi—ndi mitundu yonse ya maprogramu osawunikidwa, ndi zolaula pa msewu.

¹⁷⁹ Ndipo, O Mulungu, ndi—ndi nthawi yamisala. Ndi nthawi ya manjenje. Ndi—ndi nthawi imene munthu sangayime ndi kumvetsera, ndi kufufuza. Ndipo pansu pa zotengeka, ndi zina zotero, iwo akudzinenerabe kuti ndi Mbewu ya Abrahamu. Mulungu, momwe Inu munanenera kuti izo zikanadzachitika, mizimu idzakhala yoyandikira kwambiri mmasiku otsiriza, ndi zokopera, mpaka pafupifupi idzanyenga Osankhidwawo, ngati kukanakhala kotheka. Ndipo apa izo ziri. Mulungu, musawalole anthu awa, musalole mmodzi achite zimenezo. Chonde, Atate.

Ine ndikuwapempherera iwo, mmodzi aliyense. Mu Dzina la Ambuye Yesu, perekani izi.

¹⁸⁰ Tsopano pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ine ndikanakuchitirani inu chirichonse. Ndipo ngati ine ndimawadzudzula anthu kuti ndikhale wankhanza, Mulungu sibwenzi ali ndi ine; ine sindikuyenera kukhala pano, ine ndikuyenera kukakhala kunjya uko kwinkwake ndikudula nkhuhi kapena chinachake. Koma, abwenzi, izo—izo nzoona, fufuzani izo ndipo muwone ngati izo si Malemba. Ndipo izo zikuyenera kuti ziwululidwe mu tsiku lomaliza lino.

¹⁸¹ Tsopano kodi ndinu woonamtima mokwanira? Kodi inu mulidi, pansi pa chidutsa icho cha kunjya, kodi pali chinachake chenicheni chokhudza inu, kuti mukufuna kuvomereza kuti mwalakwitsa? Pamene mutu uliwonse ukuweramitsidwa, mtima uliwonse, ndi kudzipereka mwaulemu kwakuya, kodi mungakweze mmwamba dzanja lanu, ndikuti, “Mundipempherere ine, M’bale Branham. Ine ndalakwitsa. Mwa chisomo cha Mulungu ine ndiwongoka?” Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu. Ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, Iye amaliwona ilo. Mmakonde, Mulungu akukuonanani inu. Kwezani manja anu. Kodi inu—inu. . . Ndi zimenezotu.

¹⁸² Tsopano *apa* pali ena a inu akazi mwakhala pano ndi tsitsi lalifupi, ndipo simunakweze dzanja lanu mmwamba. Chavuta ndi chiyani ndi inu? Inu mukulakwitsa! Musayesere kuti mukakumane naye Mulungu monga choncho. Inu mudzaweruzidwa motsimikiza monga ine ndayima pa guwa lino. Inu mukutanthauza kuti mpingo wa Chipentekoste wafika mu mawonekedwe oterowo kuti iwo—iwo—iwo walimba kwambiri mpaka kuchita manyazi kuvomereza kuti walakwa? Inu musachite zimenezo. Mulungu akuchitireni inu chifundo.

¹⁸³ Ine ndikukhulupirira. Khalani ndi chikhulupiro. Ndilolani ine ndidikireno. Mulungu akudalitse iwe apo, wokonedwa. Mulungu akudalitse iwe, mlongo. Izo ndi zabwino. Ika mmwamba. . .Kuti. . .Mulungu akudalitse iwe. Uko nkulondola. Inu mukhoza kuvomereza izo tsopano; mmawa mwina zidzakhala zochedwa kwambiri, ora kuchokera pano zikhoza kukhala mochedwa kwambiri. Mulungu akudalitseni inu. Uko ndi kuwonamtima. Mulungu akudalitseni inu. Nenani, “Ine ndalakwitsa.” Zimatengera munthu weniwene kuvomereza kuti walakwitsa. Ndicho chinachake chenicheni. Mulungu akudalitse iwe, dona. Mulungu akudalitse iwe, dona. Mulungu akudalitse iwe. Uko nkulondola. Inde, mungopitirira kupemphera. Mulungu akudalitseni iwe. Ngati ine ndiphonya kuwona dzanja lanu, Iye satero. Iye amadziwa ganizo lirilonse limene liri mmalingaliro anu. Ndizo kulondola ndendende. Mulungu akudalitse iwe, ine ndikuwona dzanja lako. Izo nzabwino. Mulungu akudalitse iwe, dona wamng’ono. Mulungu akudalitse iwe, mlongo. Izo nzabwino.

¹⁸⁴ Mulungu akudalitse iwe pamenepo, dona wamng'ono. Inde, kutembenuka kwa misewu ya moyo. Zinthu zakale izi zisanawumitse mtima wako waung'ono, tembenukira kwa Mulungu tsopano, wokonedwa. Ndiko kulondola, iwe uchite zimenezo. Ine ndiri ndi mwana wamkazi wamng'ono kumeneko pafupifupi usinkhu wako. Mulungu akudalitse iwe, wokonedwa. Mulungu akudalitse iwe. Inde, Mulungu akudalitse iwe, mlongo.

¹⁸⁵ Nanga bwanji inu, m'bale? Manyazi pa inu, kumamulola mkazi wanu azichita monga chomwecho ndi kumavala zazifupi, ndi kumavala monga chomwecho ndi kumapita pa msewu. Kumadzitcha nokha mwana wa Mulungu? Kodi inu simukuzichitira nokha manyazi? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu. Uko nkulondola, vomerezani kuti mwalakwitsa. Eya. Ngati inu. . .

¹⁸⁶ “Iye amene abisa tchimo lake sadzapindula; iye amene avomereza tchimo lake adzakhala ndi chifundo.” Mulungu akudalitseni inu. Enanso? Kumbuyo mu khonde, pamwamba apo mu khonde. Iye akukuonani inu mmwamba umo. Iye amadziwa ganizo lirilonse limene liri mu mtima mwanu.

Tsopano kwezani mitu yanu miniti yokha.

¹⁸⁷ Ine ndikunena kuti alipo ena fifite kapena sikisite mu chipinda chino akweza manja awo, aang'ono ndi aakulu. Zikomo inu. Ameneyo ndi dona weniweni ndi njonda. Ine ndikukuyamikirani inu. Pali—pali ziyembekezo kwa inu pamene mukhala ololera kuvomereza kuti mwalakwitsa.

¹⁸⁸ Ine ndisanaitanire ku guwa, ine ndipempherera mipango iyi.

¹⁸⁹ Atate Akumwamba, mipango iyi ikuyimira anthu odwala, amayi ndi abambo amene akuyembekezera, ana. Nthawi ina, ife timaphunzitsidwa mu Baibulo, kuti iwo anatenga kuchokera mu thupi la Paulo Woyera mipango ndi zovala. Anthu amene anamuwona iye, anadziwa kuti Mzimu wa Mulungu unali pa iye. Paulo anakumbukira kuti Elisha anamuuza mkazi wa ku Shunemu, amene anamuuza Gehazi, “Tenga ndodo iyi ndipo ukaiyike iyo pa mwanayo.” Iye ankadziwa kuti chimene iye wagwira chinali chodalitsidwa. Paulo, iwo anatenga kuchokera pa thupi lake mipango ndi zovala, ndipo mizimu yonyansa inatuluka mwa anthu, matenda anasamuka. Tsopano, Ambuye, ife si Paulo Woyera, koma Inu mukanali Mulungu, Mulungu yemweyo.

¹⁹⁰ Tsiku lina Israeli anali pa ulendo wake mu mzere wa ntchito, akupita ku dziko lolonjzedwa. Ndipo chinachake chinawadulira iwo ku dziko lolonjzedwalo, Nyanja Yofiira. Wolemba wina anati, “Mulungu anayang'ana pansi kupyolera mu Lawi la Moto lija, ndi maso aukali, ndipo nyanja inachita mantha, ndipo iyo inafunyululira mmbuyo makoma ake ndipo

inatsegula njira yowuma kuti Israeli awolokere kupita ku dziko lolonjezedwa.”

¹⁹¹ Mulungu, pamene mipango iyi ikutengedwera kwa odwala ndi osautsika, mulole Mulungu wa Kumwamba akayang’ane pansu kupyolera mu Magazi a Mwana Wake Yemwe, mulole mdierekezi, amene akuwagwira anthu odwala amenewo, akachite mantha ndipo akachokepo pamene mipango iyi ya zizindikiro za msonkhano uno usikuuno, pamene Mawu ndi Choonadi zakwaniritsidwa; odwala ndi osautsikawo akachiritsidwe; mitima imene yasweka, ndipo ipita ku Nyumba ya Wowumba mu maminiti pang’ono; perekani kuti mdierekezi achoke, ndipo anthu awolokere kupita ku dziko la thanzi labwino limene Mulungu anawalonjeza iwo. Ine ndikutumiza mipango iyi, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa cholinga chimenecho. Amen.

¹⁹² Ndipo Mulungu akudziwa mtima wanu. Iye akudziwa chikhalidwe chanu. Kungowonetsa; ndipo ndiroleni ine ndikuuzeni inu, pali gulu lalikulu la anthu muno amene sanakweze dzanja lawo, amene amayenera kuti akweze ilo. Tsopano, ngati ine ndikuyitaneni inu kuchokera pa nsanja iyi, kunena yemwe inu munali, izo zikhoza kupweteka kumverera kwa winawake. Tsopano, inu mwandiwonapo ine ndikuchita izo nthawi zambiri. Ine ndinapeza kuti, Yesu anati, “Lolani udzu ndi tirigu zikulire limodzi. Angelo adzabwera ndipo adzamanga namsongole ndi kumuwothcha iye, poyamba.”

¹⁹³ Ndipo ndi nthawi yomanga tsopano. Aliyense wa iwo akupita mu mgwirizano wa mipingo, zipembedzo zonse. Uko nkulondola. Uko nkulondola. Mgwirizano wa Dziko, Bungwe la Mipingo, chipembedzo chirichonse chikukokera mu icho, chinthu chachikulu chikuchitika. Onsewo akubwerera ku Roma monga iwo analonjezera, “fano lopangidwira kwa chirombo,” mphamvu, chitaganya cha mipingo, ndendende basi chimene Mulungu ananena kuti chikanadzachitika. Ndi zimenezotu, akukulolani inu kumapita, ndi kumakuuzani inu kuti ndi zabwino kuchita *ichi*, ndi kuwopa kunena chirichonse za icho, kuwopa kuti ziwononga tikiti ya chakudya kwinakwake.

¹⁹⁴ Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, m’bale wanga, mlongo, Mulungu awulule kwa inu kuti ine ndimakukondani inu. Sikuti ndikufuna kukhala wosiyana; ndi kukhala wona. Musatengerepo mwayi umodzi. Inu simungadutse kuwala kofiira, chifukwa cha thupi lanu. Nanga bwanji solo yanu? Musadutse limodzi la magetsi ofiira a Mulungu.

¹⁹⁵ Ena a inu mukudwala. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Winawake amene wasimidwa mu chinachake, mungokhala ndi chikhulupiro. Ine ndikuwonetsani inu ngati Iye ali weniweni, ngati chiri Choonadi kapena ayi. Abrahamu,

inu mukukumbukira Mngelo anabwera kwa iye ndi chimene Iye anachita? Muwone ngati chiri chinthu chomwecho.

¹⁹⁶ Apa pali dona wamng'ono wakhala pomwe pano, pomwe pano, iye ali ndi khansa. Iye ali ndi chotupa, ndipo akukonzekera opareshoni. Iye akundiyang'ana ine tsopano, ndi mikanda yofiira imeneyo kuzungulira khosi lake. Ndiwe wochokera ku Portland. Koma ngati iwe ungatero. . . Ngati ndiko kulondola, kweza mmwamba dzanja lako. Uko nkulondola. Mukuona? Ine sindimakudziwa iwe, ndife alendo. Koma izo nzoona. Tsopano ungakhale bwanji pamenepo, ndi chikhulupiriro chokwanira kuti ukhudze chovala cha Khristu pamene Mngelo wa Kuwala uja abwera pa iwe monga choncho, chisomo cha Mulungu? Landira Izo, dona. Khulupirira Izo. Osati izo zokha, koma ukhulupirire Uthenga wonse.

¹⁹⁷ Apa pakhala mkazi wakhala kumbuyo komwe kuno. Tayang'ana apa, dona. Ukuvutika ndi vuto la matumbo. Ukhulupirire ndi mtima wako wonse. Inde, ndiwe mlendo kwa ine. Ukhulupirire ndi mtima wako wonse, ndipo ukhale bwino.

¹⁹⁸ Pali mwamuna wakhala pafupi ndi iwe, akuyenera azipita kwawo. Iye sangakhale motalika. Ali ndi vuto ndi makutu ake. Ali ndi vuto ndi a. . . Anali ndi chimfine, ndipo chinayambitsa chifuwa. Iye akulephera kuthana ndi zimenezo, izo—izo ziri ngati a—zovuta zambiri ziri mmenemo. Uko nkulondola, bwana. Inu mumagwira ntchito pa mtundu wina wa makina ngati mizinga kapena chinachake chonga izo. Inu mukuyenera kubwerera ku ntchito yanu. Ndine mlendo kwa inu. Ngati zinthu zimenezo ziri zoono, kweza mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Ngati inu muli ndi chikhulupiriro chokwanira kuti mumukhudze Ambuye Yesu, bwanji osakhala mwamuna weniweni ndi kukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse?

¹⁹⁹ Pali dona wakhala kumbuyo uko, iye ali ndi mtundu wina wa nthenda yapakhungu mmanja mwake. Iye sakudziwa nkomwe chimene iyo ili. Dokotala samadziwa nkomwe chimene iyo ili. Iye wakhala nayo iyo kwa zaka ndi zaka. Oh, iye ayisowa iyo, motsimikiza monga dziko. Abiti Daniels, McDaniels. Ndi zimenezotu. Ida McDaniels, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Ine sindikumudziwa mkaziyo, sindinamuwonepo iye. Koma apo pali Kuwala pamwamba pa iye.

²⁰⁰ Icho ndi chiyani? Iye amakudziwani inu! Ndipo Iye akudziwa kuti inu mukulakwitsa! Mulungu yemweyo amene akuyankhula kupyolera mwa ine mwanjira iyi, akuyankhula kupyolera mwa ine kupyolera mu Mawu.

²⁰¹ Tsopano, aliyense muno amene akuzindikira Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo kudziwa kuti mwakhala mukulakwitsa, tiyeni tibwere ku guwa tsopano. Bwerani kuno miniti yokha, mundilole ine ndikupempherereni inu. Ngati mukudziwa kuti mwakhala mukulakwitsa, mukufuna kuvomereza kuti mwalakwitsa.

Inu mukufuna kuti mukhale Mkhristu weniweni kuyambira pano mpakana, bwerani kuno mudzazungulire guwali. Ine sindikufuna basi kuti nditchule dzina lanu, izo—sizingakhale za Chikhristu. Mmwamba umo pa khonde, bwerani mpaka mmusi, uwu ndi mwayi wanu. Bwerani kuno tsopano! Bwerani ku guwa, nenani, “Ine ndikubwera, Ambuye.” Wochimwa, iwe upange njira yako yobwera ku guwa, uwu ukhoza kukhala mwayi wako wotsiriza. Kodi inu simubwera tsopano pamene ife. . . limba likuyimba mokongola, “Ine ndikubwera, Ambuye, ndikubwera tsopano kwa Inu.” Chabwino, aliyense ayimbe tsopano.

Ine ndikubwera, Ambuye!
Ndikubwera tsopano kwa Inu!

²⁰² Kodi inu simubwera? Tsikani kuchokera pa khonde, bwerani pansi. Bwerani kuno. Nanga bwanji inu, anthu inu amene mumadzinerera kuti ndinu Akhristu, Mbewu ya Abrahamu? Mulungu akudalitseni inu, akazi. Mulungu akudalitseni inu, alongo anga. Inde. Mulungu ndithudi alemekeza izo. Ndinu owonamtima. Mwinamwake abusa anu alephera kukuuzani inu zimenezo. Mupite kwanu ndipo mukatenge Baibulo lanu, ndipo mukafufuze ngati izo ziri zoonu, kapena ayi. Inu mukudziwa kuti ndi zoonu, ine ndisananene ngakhale chirichonse. Inu akazi Achipentekoste, inu simungazipake penti kwa chirichonse. Mulibe chirichonse mu Baibulo chokhudza kudzipenta; Yezebeli yekha, iye anadziphoda nkhope yake ndi zinthu, ndi penti ndi zinthu. Koma ziripo mu Baibulo za inu muli ndi tsitsi lalitali, “Ndi chinthu chachilendo kuti mkazi azipemphera ngakhale ndi mutu wake wodulidwa, tsitsi lometedwa.”

. . . kwa Inu!

²⁰³ Inu mukufuna kuti muyanjanu ndi Mulungu, mu Kukhalapo pamene Iye ali pano? Bwerani! Dzaimirireni, mudzapange kuyima ndi Iye! Muimirire ku mapazi anu ndipo mubwere kuno, ndikuti, “Ine ndikubwera. Ine—ine ndipanga chiwonetsero. Ine ndikufuna dziko lonse lidziwe kuti ine ndikulakwitsa, ndipo ine ndikufuna kuti ndikhale wolondola pamaso pa Mulungu.” Kazibwerani tsopano!

Ine ndikubwera, Ambuye!
Ndikubwera tsopano kwa Inu!
Ndisambitseni, ndiyeretseni ine mu Magazi
Amene anayenderera kuchokera ku Kalvare.

Kenanso, aliyense!

Ine ndikubwera. . .

Bwerani. Alipo ochuluka kunja uko, kumbukirani. Inde, uko nkulondola.

. . . ine, ndiyeretseni Mmagazi Anu
Amene anayenderera kuchokera ku Kalvare.

²⁰⁴ Pali anthu akubwerabe, mungopitiriza kumapemphera. Tsopano, abwenzi, ine ndiribe zochuluka zoti ndikukakamizeni. Ine ndikukhulupirira Mawu amagwira ntchito Yake pamene Iwo akupita kunja uko. Musawukwiyitse Mzimu Woyera. Ukhoza kukhala mwayi womaliza umene mungakhale nawo; ine ndikudalira kuti sichoncho. Inu mukudziwa chimene icho chimachita kukuwonani inu pamene mukuvomereza kuti mukulakwitsa? Izo zimanena kwa ine kuti pali chinachake chenicheni pamene, chimene inu mukufunadi kuti muchichite molondola. Tsopano ndi limba lokha, mwapang'onopang'ono ngati mungathe, pamene ine ndikuyankhula. Kazibwerani, anthu, musingobwerabe kuno. Ine ndikufuna kuti muzibwerabe. Kodi mukudziwa zimene anthu awa achita? Ambiri a awa ndi mamembala ampingo olembedwa, ndipo akudziwa kuti ndanena Choonadi.

²⁰⁵ Osati *ine*. Basi ngati pamene Mose anapita kumeneko kukawauza anthu za Ambuye; ndipo Ambuye, pansi pa Lawi la Moto lija, anawatsimikizira Mawu ndipo anasonyeza kuti Iwo anali olondola. Lawi la Moto lomwe lija liri pomwe pano ndi ife. Ndi Khristu yemweyo, akuchita chinthu chomwecho kwa m'badwo wa Amitundu, monga Iye analonjeza kuti adzachita.

²⁰⁶ Kodi zimenezo zikundipangitsa ine kukhulupirira chiyani? Kutu ndinu weniweni mu mtima mwanu. Chinakupangitsani kuti muimirire pa mapazi anu ndi chiyani? Chifukwa Chinachake chinali pafupi ndi inu, chimene chinati, "Mukulakwitsa." Tsopano ameneyo anali Mulungu, chifukwa ena a inu mumachita manyazi kuyima pano monga choncho pamaso pa anthu, mutatha kuvomereza. Koma izo zimawonetsera kuti Chinachake chenicheni ichi Chimene chinati, "Mukulakwitsa," ndipo Icho chinabwera ndi Mawu, kupyolera mu kuzindikira zamumtima. Kudzera . . .

²⁰⁷ Kodi mphatso izi zimatuzidwiranji ku mpingo? Kodi mphatso yoyamba ndi chiyani? Chinthu choyamba ndi chiyani? Atumwi (omwe ali amishonare), aneneri, aphunzitsi, abusa, avangeli. Iwo palimodzi ndi wopangitsa Mpingo ungewiro.

²⁰⁸ Ndipo kodi Mawu a Ambuye amabwera kuti, kwa ndani? Mawu a Ambuye ankabwera kwa mneneri, nthawizonse, sankakaikiridwa nkomwe. Osati mphatso ya uneneri; mphatso ya uneneri imakhala pa mmodzi, ndipo kenako pa wina. Mneneri amabadwa, wokonzedweratu ndi Mulungu. Yesu Khristu anali Mwana wa Mulungu, Mwana wokonzedweratu wa Mulungu. Yesaya anamuuza Yohane, Yohane M'batizi, zaka seveni handiredede ndi thwelofu iye asanabadwe, iye anali "mawu a wofuula mchipululu." Mulungu anamuuza Yeremiya, "Iwe usanawumbidwe nkomwe mmimba mwa amayi ako, ine ndinakudziwa iwe ndipo ndinakuyeretsa iwe, ndipo ndinakudzodza iwe mneneri kwa mafuko." Ndipo pamene muwawona aneneri akuwonekera, chiweruzo chiri pafupi.

209 Tsopano, “Chiweruzo chimayambira Mnyumba ya Mulungu, ndi anthu a Mulungu.” Tsopano ife talakwitsa! Ife tachita zolakwika. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti iwo akhala pano usikuuno, ndizo Mbewu ya Abrahamu ndipo yokonzedweratu kwenikweni ku Kuwala kwa Mulungu kuti iwalire pa iyo; pamene Kuwala kukhudza iyo, iyo idzayima. Pali chinachake chimene chikuyenera kuchitika, inu muli pamenepo! Tsopano inu muli pano, tiyeni tiweramitse mitu yathu ndi kuvomereza zolakwa zathu.

210 Mzanga wochimwa, ngati iwe waima mu gulu lino pano, chimene alipo ena, manyazi pa inu; koma madalitso kwa iwe tsopano, iwe wavomereza izo, wakhulupirira izo ndi mtima wako wonse.

211 Inu Akhristu, akazi inu amene mukudziwa, ine ndikukhulupirira ndinu akazi abwino. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Mulungu akhoza kufotokoza kumverera kwa mtima wanga kwa inu. Ine sindikufuna kuti ndikhale wankhanza kwa iwe, mlongo; ine ndiri ndi mkazi, nanenso, ndi awiri—atsikana awiri achichepere. Ine ndimakukonda iwe ngati mlongo wanga.

212 Ndipo, m’bale, ine sindimafuna kuti ndipweteke kumverera kwanu, koma nthawizina kugwedeza pang’ono ndi Mawu kumakuthandizani inu.

213 Tsopano, ngati ife talakwitsa, tiyeni tinene kuti ife talakwitsa. Ndipo chiripo—chiripo chisomo, chochuluka, cha ife usikuuno. “Iye amene adzavomereza zolakwa zake, padzakhala chifundo kwa iye. Iye amene adzabisa tchimo lake, sadzapindula konse.” Tchimo lanu ndi chiyani? Kusakhulupirira kwanu. Ngati mukulibisa ilo, kunena kuti, “Chabwino, ndine wabwino basi monga ena onsewo.” Inu mukulakwitsa. Ndipo inu simudzasanthira chitsogolo chirichonse kuposa momwe mukusunthira pano. Mukakhala mwanjira imeneyo, inu simudzapita patsogolo paliponse mpaka mutadzawoloka chotchinga icho ndi kukonza izo. Kumbukirani, inu simungakhoze kuchita zimenezo; inu mudzayenera kuyenda pa Mawu a Mulungu.

214 Ndipo bola ngati inu muli moyo, inu nthawizonse mudzakhala mukukumbukira izi. Tsiku lalitali kwambiri limene mudzakhale moyo, inu mudzakumbukira usikuuno. Kumbukirani, ine ndikukuuzani inu **PAKUTI ATERO AMBUYE!** Ine ndinakhala mu nkhalango madzulo ano, ndikupemphera, Iye anayankhula ndi ine zokhudza izi pano, anati, “Ukanene izo ndipo ukatchule izo, ndipo Ine ndikakuchitira iwe chinachake.” Ndipo ndi izi apa.

Tsopano tiyeni tipemphere.

215 Atate Akumwamba, molemekeza ndi moonamtima payima ochimwa mwa omvetsera awa pakali pano. Iwo

adzuka pa mpando wawo ndipo ayenda kubwera kuno, kuti adzangopanga kuvomereza. Pali Akhristu amene abwera, akupanga kuvomereza kwawo.

²¹⁶ Apa pali alongo aang’ono ofunika amene Kuwala kuwalira pa iwo, pansu mu mtima mwawo iwo amadziwa kuti iwo amalakwitsa, iwo amadziwa kuti Baibulo limaphunzitsa zinthu zimenezo, ndipo iwo ndi ololera kuti azisiye zonsezo.

²¹⁷ Apa pali abale ayima apa, abale ofunika, ana aamuna a Mulungu wamoyo, amene, kupyolera mu kachikhulupiriro ndi zikhaliidwe zofunda, anasochera kulowa mdziko. Iwo akubwerera usikuuno, Atate. Iwo akubwerera. Iwo ali, apa iwo ali.

²¹⁸ Tsopano, Atate, ife tikuzindikira kuti pamene iwo anayima pa mapazi awo, iwo anaswa; asayansi onse, ananena kuti simungathe kusuntha, mwagwiridwa pansu. Koma pamene iwo anakweza manja awo ndi kuyenda kubwera kuno, iwo anatsimikizira kuti munali Mzimu mwa iwo umene ukanakhoza kupanga lingaliro. Iwo apangira izo kwa Khristu.

²¹⁹ Yesu, apa pali Mawu Anu Omwe, ndipo ine ndingowabwerezera iwo kwa Inu.

²²⁰ Ine ndikukupatsani Inu anthu awa usikuuno, ngati wantchito Wanu. Ine ndachita basi monga momwe Inu munandiuzira ine kuti ndichite, lero mu nkhalango, ndipo apa pali ndendende basi zimene Inu munati zikanadzachitika. Ndipo pali mboni za zinthu zimenezo, zitayima apa. Kuti mutsimikizire Kwanu—Kukhalapo Kwanu, Inu munapita pa omvetsera, kuwauza anthu za chimene iwo ali ndi kumene... iwo achita, ndi zina zotero, kuwadziwa anthuwo, maina, ndi chimene iwo ali ndi chimene iwo achita, chimene chalakwika.

²²¹ Ndipo tsopano Inu munanena mu Mawu Anu, kuti, “Iye amene adzandivomereza Ine pamaso pa anthu, ameneyo Ine ndidzamuvomereza pamaso pa Atate Anga ndi Angelo overa. Iye amene adzachita manyazi ndi Ine pamaso pa anthu, ameneyo Ine ndidzamuchitira manyazi pamaso pa Atate Anga ndi Angelo overa.” Tsopano alongo awa ndi abale awa ayima usikuuno pamaso pa mamembala awo ndi azibusa awo, ndi okondedwa awo, kudzanena kuti—kuti iwo sakuchita manyazi ndi Inu, koma iwo akuchita manyazi ndi momwe iwo achitira. Tsopano ine ndikutsimikiza, Ambuye, kuti Inu muwakhululukira iwo. Inu munalonjeza izo. Inu munati, “Iye amene adzavomereza machimo ake, ali ndi chifundo.” Ndipo iwo akuvomereza izo, ndipo iwo apeza chifundo. Ndipo Inu Amene mukhoza kuchiritisa odwala, ndi kuti, “Kodi izo sizophweka kunena, ‘Machimo ako akhululukidwa kwa iwe,’ monga momwe ziriri ‘Yalula mphala yako nuyende?’”

²²² Ine ndikuwatenga awa. Ine—ine ndikumutenga aliyense wa iwo, Ambuye. Ine ndayesetsa kukuimirani Inu zaka zonsezi,

ndi Mawu Anu. Ndipo iwo akuimirani Inu usikuuno, ndipo ine ndikuwatenga iwo. Ine ndikuwachotsa iwo mu nsagwada za dziko, ndipo ndikuwapereka iwo kwa Inu, Ambuye Yesu. Iwo ali zikho za Uthenga usikuuno, za Mawu a Mulungu. Asungeni iwo, Mulungu Wamphamvuzonse, pansi pa Mphamvu Yanu Yoyera. Mulole iwo akakule, mulole Kuwala kwa Mulungu kuwalire mmoyo wawo. Mulole amuna awo ndi akazi, Ambuye, ayambe kukula mu mphamvu ndi nyonga ya Mzimu Woyera. Mulole chinachake chichitike chimene chiti chidzasinthe mipingo yawo yonse ndi—ndi dera lonse loyandikana kumene iwo aliko. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, iwo ndi Anu. Iwo—iwo ndi zikho za msonkhano usikuuno, za Mawu amene alalikiwa. Ine ndikutenga moyo wawo, mu Dzina la Yesu Khristu. Ine ndikufuna ndidzakomane nawo iwo mbali inayo, pamene iwo adzakhale achisavundi, atabwereranso kudzakhala mnyamata ndi atsikana kachiwiri, ndi kukhala achichepere ndi okondeka kwanthawizonse. Iwo ndi Anu, Atate. Iwo ndi zikho zimene Mulungu wapereka kwa Mwana Wake, Khristu Yesu, mwa mphamvu ya Kukhalapo Kwake ndi Mawu a Mulungu. Iwo ndi Anu, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu; ndipo ndikuwatenga moyo uliwonse, moyo uliwonse umene wayima pano. Kuvomereza kulikonse kwalandiridwa, tchimo lirilonse lakhululukidwa.

²²³ Ndipo aliyense amene wayima pano, ine—ine—ine ndikupempherera mphamvu ya Mzimu Woyera mwa iwo, kuti ichite, ichite icho chimene chiri choyenera, kuwathandizira iwo mu ora la mdima lino pamene dziko ladzaza ndi zokongola. Ndipo, O Mulungu, mudzandithandize ine mawa usiku, kuti—kuti ndidzazibweretse izo moyera ndi momveka kwa iwo, Ambuye; ndi kumasulidwa ku kukongola kwa dziko lino, kuti iwo akakhale okonzeka kuti adzakomane ndi Khristu pa nthawi ya Kudza Kwake. Perekani izi, Atate. Ife tikukukhulupirani Inu tsopano.

Ndipo tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa.

²²⁴ Aliyense wa inu amene wayima pamapazi anu, ine sindikukhulupirira kuti inu mwabwera kudzafufuza, chifukwa inu mwabwera pansi pa kulalikirira kolimba, kovuta kwa Uthenga, wodula. Koma inu mukukhulupirira kuti Yesu ananena kuti, “Palibe munthu angadze kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye, ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzadza.” Tsopano awo ndi Mawu otsimikiziridwa a Mulungu. Iye anamuuza Abrahamu, Iye analonjeza ndipo analumbirira ku lumbiro, ndipo apa inu munamva Liwu la Mulungu usikuuno ndipo mwabwera pa maziko amenewo. Inu mukuyenera kukhululukidwa! Ndipo nonsenu muovomereze izo ndi kukhulupirira kuti Mulungu wakukhululukirani inu zolakwa zanu, ndipo kuyambira usiku uno mpakana mtsogolo, mwa chisomo cha Mulungu, inu mudzamkhalira Iye moyo

masiku amoyo wanu wonse, ndipo mudzachita chirichonse chimene Baibulo ili limaphunzitsa kuti inu muzichita, ndipo mudzakhulupirira kuti Mulungu akukupatsani inu chisomo kuti muzichita izo tsopano, pokukhululukirani inu zakale zanu; munakweza dzanja lanu, ndikuti, “Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse.” Mulungu akudalitseni inu.

²²⁵ Akhristu nonse kunjā uko amene mukuwanyadira iwo, nenani, “Mulungu alemekezeke, chifukwa cha iwo!” [Osonkhana akuti, “Mulungu alemekezeke, chifukwa cha iwo!”—Mkonzi]. Tiyeni tinene izo kachiwiri. “Mulungu alemekezeke, chifukwa cha iwo!”

Tsopano tiyeni tiyime pa mapazi athu, aliyense. Ine ndikufuna poyambira pa:

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa Kalvare.

²²⁶ Tiyeni tonse palimodzi tsopano, aliyense tiyimbe iyo ndi manja athu mmwamba. Chabwino.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

²²⁷ Kodi inu simukumverera kuti mwakhulidwa kwenikweni? Kodi Mawu samakukhulani inu ndi kukupangitsani inu kumverera bwinoko? Sichoncho izo?

²²⁸ Inu simukundikhulupirira ine kuti ndine a—a—wabodza, sichoncho inu? Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine Choonadi? [Osonkhana akuti, “Ameni!”—Mkonzi].

²²⁹ Ine ndikumuyang’ana pakali pano Mngelo wa Ambuye uja Amene ine ndimamuyang’anira pa anthu, wazungulira mozungulira gulu ili limene layima pomwepa mu maonekedwe a mtanda. Mulungu Kumwamba! Chithunzi chomwecho inu. . . Mngelo amene mumamuwona pa chithunzi icho, ali pomwe pano pa gulu ili la anthu, akungoyenda mozungulira, ine ndikungomuyang’ana Iye, kuchoka pa malo kupita pa malo. Ine ndikukhulupirira, ngakhale, kuti nthenda iliyonse imene yaima mu gulu limenero yapita. Ine—ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse, kuti tchimo lirilonse lakhululukidwa.

²³⁰ Tiyeni basi—tiyeni tingogwirana chanza wina ndi mzake pamene tikuyimba “Ine ndinkonda Iye.”

Ine . . .

Nenani, “Ambuye alemekezeke!” [Osonkhana akuti, “Ambuye alemekezeke!”—Mkonzi].

. . .nkonda Iye, ndinkonda Iye

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

²³¹ Tsopano tiyeni tingomutamanda Iye, tinene, “Ambuye alemekezeke! Zikomo Inu, Ambuye Yesu.”

Ife tikukuthokozani Inu, Ambuye, chifukwa chowabweretsa anthu muno, chifukwa cha Mawu Anu. Iwo ndi akuthwa ngati lupanga lakuthwa konsekonse, koma Iwo amazindikira malingaliro a mtima. Iwo amatsimikiza izo. Iwo amadula dziko, mnofu, zinthu zachidziko kuzichotsa kwa anthu, ndi kuwapanga iwo kukhala zolengedwa zatsopano mwa Khristu. Momwe ife tikukuthokozerani Inu, Atate! Ife tikukutamandani Inu ndi mtima wathu wonse. Zikomo Inu chifukwa cha iwo, Ambuye. Mulole iwo adzazidwe ndi Mzimu! Mulole Mzimu Woyera ungowatengera iwo mu ulamuliro Wake, ndipo mulole kuti payambike chitsitsimutso chachikale pakati pa mipingo iyi, Ambuye, chimene chidzangosesa monse kudutsa mmadera, kulikonse pamoto ndi mphamvu ya Mulungu. Titumizireni ife pentekoste yeniyeni, Ambuye, mphamvu yeniyeni ya Mzimu kubwerera mmiyoyo ya anthu. Perekani izi, Atate.


²³² Iwo ndi Anu. Mwa chisomo cha Mulungu, iwo ndi Anu. Iwo ndi Mbewu ya Abrahamu, mogwirizana ndi lonjezo. Perekani izi, Ambuye. Iwo amakhulupirira Mawu Anu; chirichonse chotsutsana, ngati kuti panalibepo. Iwo amakhulupirira Mawu chifukwa iwo ndi Mbewu ya Abrahamu. Iwo ndi Anu, Atate, Mpingo wokonzedweratu kuti udzawale mu tsiku lotsiriza. Zikomo Inu, Atate, chifukwa cha iwo.

Ndinkonda Iye . . .

Kwezani manja anu tsopano pomutamanda Iye.

Ine . . .

Mmwamba mmakonde! Uko nkulondola.

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Ndipo . . . 

62-0705 Yehova-Yire #1
Municipal Auditorium
Grass Valley, California U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org